

KUPHUNZIRA MALEMBA A M'BAIBULO

M'mene mungawerengere mau a Mulungu ndi kuwamvetsa

Bukhuli analipanga moganzira zofuna za abusa ndi atsogoleri a mipingo

Bukhuli linatsindikizidwa ndi:

INTENSIVE CARE MINISTRIES,
P.O. Box 109, Mentone, California 92359 USA (909) 798-0451
Email: info@icmbible.org
www.icmbible.org

COPYRIGHTED MATERIAL
All Rights Reserved
Rev.11/08

ZOMWE MUNGAFUNE KUDZIWA ZA BUKHULI

Pastor Dan Finfrock, analemba bukhuli atagwira ntchito ndi abusa komanso atsogoleri a mipingo kwa zaka zambiri mdziko la Philippines. Cholinga chake ndikuthandiza atsogoleri kuphunzira kuwerenga ndi kumvetsa Baibulo popanda kudalira mabuku ena a padera othandizira kumvetsa Baibulo omwe samapezeka mosavuta m' maiko omwe akukwera kumene.

Bukhuli limaphunzitsa atsogoleri kutanthauzira mau a Mulungu moyenera komanso momveka bwino. Iyi ndi njira yosavuta komanso yatsatanetsatane yowerengera ndi kumvetsa mau a Mulungu.

Bukhuli lingagwiritsidwe ntchito kuphunzitsa wina aliyense yemwe ali ndi chidwi chophunzira kuwerenga ndi kumvetsa bwino mau a Mulungu. Bukhuli likugwiritsidwa ntchito m' maiko ambiri ndipo latanthauziridwa mu zinenero zoposa makumi atatu ndi mphambu zisanu pa dziko lonse.

CHIDZIWITSO

Bukhuli lingakuthandizeni bwino mukaligwiritsa ntchito pamodzi ndi CD kapena DVD yathu.

MLEMBI WA BUKHULI

Mlembi wa bukhuli, Pastor Dan Finfrock anakulira mu mpingo wa Alliance Church ku California mdziko la Amerika. Iwo anaphunzira ku Simpson Bible College ya mpingo-wo. Atamaliza maphunziro awo ku sukulu ya ukachenjede ya Redlands anayamba kuphunzitsa magulu a m'sukulu za ukachenjede zosiyanasiyana kuwerenga ndi kumvesetsa bwino mau a Mulungu. Kenaka Pastor Finfrock analowa ubusa ndipo anatomikira mipingo isanu. Mpingo omaliza kutumikira unali wa Calvary Chapel ku Banning, mdziko lomwelo la Amerika.

Mchaka cha 1985, Pastor Finfrock ndi banja lawo anapita mdziko la Philippines komwe anakayambitsa mpingo wa Intensive Care Ministries. Iwo anawona kuti kunali kofunika kuphunzitsa abusa a m'dzikolo kawerengedwe ka mau a Mulungu ndipo potero anazindikira kuti abusa-wo amaphunzira msanga pogwiritsa ntchito njira yomwe ili m'bukhu lino. M'chaka cha 1991, iwo ndi banja lawo anabwerera mdziko la Amerika komwe anayamba kukhazikitsa ntchito-yi m'maiko ambiri. Pastor Finfrock amayenda m'maiko ambiri omwe akukwera kumene ndipo akhala akugwira ntchito mdziko la Russia kwambiri zaka khumi ndi ziwiri zapitazi. Mpingo wa Intensive Care Ministries uli ndi atumiki ochokera mdziko la Russia khumi omwe akutumikira m'maiko osiyanasiyana. Pastor Finfrock amakhala ku Mentone, California, mdziko la Amerika ndi mkazi wawo Debbie komanso mwana wawo wamwamuna omaliza Aaron. Iwo ali ndi ana ena atatu omwe ali pa banja, Nathan, Lela, Corrie komanso ali ndi zidzukululu zisanu ndi chimodzi.

MPINGO WA INTENSIVE CARE MINISTRIES

CHIKHULUPILIRO CHATHU

1. Timakhulupilira kuti Mulungu amakonda aliyense ndipo chifukwa cha chikondi chake, anatumiza mwana wake Yesu kudzafa pa mtanda chifukwa cha machimo a anthu ndipo Yesu anadzutsidwa kwa akufa pa tsiku lachitatu.
CHONCHO: Timavomereza ndi kupangira umboni kukhululukira kwa machimo komanso kuuka pa mtanda kwa Ambuye.
2. Timakhulupilira kuti Baibulo ndi mau a Mulungu ndipo ndi chinthu chopindulitsa kuphunzitsa mau-wa ndi cholinga cholimbikitsana, kubwezana ngati wina akusokonekera komanso kulimbikitsana m'choonadi kuti mtumiki wa Mulungu akhale ndi zida zomuyenereza kugwira ntchito yabwino. 2 TIMOTEO 3 ndime 16 ndi 17.
CHONCHO: Timalimbikitsa kuphunzitsa mau a Mulungu.
3. Timakhulupirira kuti Mulungu anasankha amuna ndi akazi ena mwapadera ndi cholinga cholimbikitsa mpingo wa khristu kuti ukhwime ndi kukula mwa Khristu. AYEYESO 4 ndime 11 mpaka 16.
CHONCHO: Timasakasaka amuna ndi akazi omwe ali ndi mphanso zapadera ndi kuwaphunzitsa kaphunzitsidwe ka mau a Mulungu.
4. Timakhulupilira kuti ambuye ndi mpulumutsi wathu Yesu Khristu abwera posachedwa.
CHONCHO: Timapita ndikukapanga atumiki m'mitundu yonse. MATEYO 28 ndime 19.
5. Timakhulupilira kuti pali thupi limodzi lokha la Khristu ndipo ngakhale pali kusiyana pa mipingo yake, tonse ndi amodzi kupyolera mu ntchito za mzimu woyera.
CHONCHO: Ndife okhulupirika kulimbikitsa umodzi wa mzimu woyera AEFESO 4 ndime 3

MASOMPHENYA ATHU

Mpingo wa Intensive Care Ministries anaukhazikitsa ndi cholinga chophunzitsa abusa ndi atsogoleri a mipingo kugwira ntchito ya Ambuye. Zolinga zathu ndi ziwiri:

1. Kuwaphunzitsa kuwerenga ndi kumvetsa bwino mau a Mulungu komanso
 2. Kuwapatsa chidwi chodyetsa nkhoa zawo chakudya chabwino cha moyo wa uzimu kupyolera mu njira za dongosolo zophunzitsira mau a Mulungu.
- Masomphenya athu ndi kukhazikitsa maphunziro-wa m'maiko ambiri kuti tikwaniritse zolinga zathu-zi.

ZA MKATIMU


KAKONZEDWE KA MAPHUNZIRO

Mau olembedwa m’Baibulo

1. Ndime zolongosola
2. Makalata a Atumwi
3. Mafanizo
4. Ndakatulo
5. Zolosea

↓
Sankhani mfundo zikuluzikulu pa ndime yomwe mwawerenga

NDONDOMEKO



PHUNZITSANI MAU ONSE A M’BAIBULO

Kumbukirani mau omwe Paulo anaphunziitsa potsanzikana ndi atsogoleri a ku Efeso
“Popeza sindinabise kwa inu uphungu wonse wa Mulungu.”

MABUKU OMWE AMAKAMBA ZA LAMULO LA MOSE

- Genesis
- Ekisodo
- Levitiko
- Numeri
- Deteronomo

MABUKU OMWE AMAKAMBA ZA UTHENGA WABWINO WA YESU

- Mateyo
- Mariko
- Luka
- Yohane

MABUKU AMENE AMAFOTOKOZA MBIRI

- Yoswa
- Oweruza
- Rute
- 1 Samuel
- 2 Samuel
- 1 Mafumu
- 2 Mafumu
- 1 Mbiri
- 2 Mbiri
- Ezra
- Nehemiya
- Estere

MABUKU A NDAKATULO

- Yobu
- Masalimo
- Miyambo
- Mlaliki
- Nyimbo ya Solomo

MAKALATA A ATUMWI

- Aroma
- 1 Akorino
- 2 Akorinto
- Agalatiya
- Aefeso
- Afilipi
- Akolose

- 1 Atesalonika
- 2 Atesalonika
- 1 Timoteo
- 2 Timoteo
- Tito
- Filimoni
- Aheberi
- Yakobo
- 1 Petulo
- 2 Petulo
- 1 Yohane
- 2 Yohane
- 3 Yohane
- Yuda

ALOSI AKULU

- Yesaya
- Yeremiya
- Maliro
- Ezekiel
- Daniel

MABUKU OLOSERA

- Chivumbulutso

ALOSI ANG'ONO

- Hoseya
- Joel
- Amosi
- Obediya
- Yona
- Mika
- Nahum
- Habakuk
- Zefeniya
- Hagayi
- Zakaliya
- Malaki

MABUKU A M'BAIBULO

NJIRA ZOPHUNZIRIRA BAIBULO

Njira zitatu zomwe amazigwiritsa ntchito kwambiri pophunzira Baibulo ndi:

KUMVETSA M'MENE ZINTHU ZIMAYENERA KUKHALIRA

.....ndikusanthula mfundo zomwe zingatithandize kulongosola pa zomwe tikuwona

KUYAMBIRA ZOMWE TIKUDZIWA.....Kuyambira pa mfundo yomwe tikuyidziwa bwino ndikufotokoza m'mene zinthu zikuyendera

KUYAMBIRA PA MFUNDO YAYING'ONO

NKUMACHULUKITSA.....Kugawana maganizo

TANTHAUZO LA

KUMVETSA	KUTANTHAUZIRA	KUCHITA ZOMWE TAPHUNZIRA
-----------------	----------------------	---------------------------------

KODI MAU AKUTI CHANI?

- Werengani ndime kangapo
- Lembani zomwe mwaganiza kuti ndi tanthauzo la ndime-yo pomwe munawerenga koyamba
- Lembani akukhudzidwa mu ndimeyo, akukhudzidwa bwanji, zinachitika liti, zinachitika kuti, zinachitika bwanji?

TANTHAUZO LA

KUMVETSA	KUTANTHAUZIRA	KUCHITA ZOMWE TAPHUNZIRA
-----------------	----------------------	---------------------------------

KODI MAU AKUTI CHANI?

- Tanthauzirani m'mene mukumvera
- Werenganinso molabadira zomwe ndimeyo ikufuna kunena
- Lekani mau atanthauzire mau
- Chipangano chatsopano chikhale patsogolo

ZINA ZOMWE ZINGAKUTHANDIZENI KUTATANTHAUZIRA MAWU

Pofuna kumvesetsa mau a Mulungu bwino lomwe ndi koyenera kutsatira miwuni ina yomwe ingakuthandizeni. Kutsatira miwuni iyi sikukutanthauza kuti ndiye kuti nthawi zonse muzitanthauzira mawu moyenera koma kusatsatira miwuni-yi kumapangitsa kulakwitsa potanthauzira mawu nthawi zambiri.

Nawa malamulo ena amene samalabadwiridwa nthawi zambiri

I. TANTHAUZIRANI ZOCHITIKA NDI MAWU A MULUNGU OSATI KUTANTHAUZIRA MAWU A MULUNGU NDI ZOCHITIKA

Pamene anthu atanthauzira mawu ndi zochitika m'moyo mwawo, zochitika m'moyo mwawo-zo amaziyika patsogolo pa mawu a Mulungu. Dziwani kuti mau a Mulungu ali patsogolo ndipo miyoyo yathu ili pansu pa ulamuliro wa mau a Mulungu.

Pamene m'khristu agwiritsa ntchito mlingo kwa ena womwe unagwira ntchito kwa iye, iyeyo ali pa chiopsezo cholakwitsa ubwino wa mlingo-wo, ngakhale mlingo-wo ndi othandiza malinga ndi malamulo a m'Baibulo. Chitsanzo pa nkhanayi ndi munthu amene amakomana ndi mavuto chifukwa chogula zinthu pa ngongole ndipo anapanga chisankho chosiya kugula zinthu pangongole. Munthuyu anakwaniritsa kuthetsa vuto lake mpaka anayamba kuwumiriza anthu ena kuti asiye kugula zinthu pa ngongole chifukwa kutero ndikulakwira mawu omwe amati, "Usatenge chinthu cha mwini..." (Aroma 13 ndime 8). Apa munthuyu watanthauzira mau a Mulungu pogwiritsa mlingo wa iye mwini ndipo wayika zochitika za m'moyo wake patsogolo pa mau a Mulungu.

II. MUSAWERUZE PAMENE MAWU A MULUNGU SAKUTERO

Pali ndime zambiri m'mene Baibulo siliweruza. Musakopeke kusayankhula zomwe Baibulo silikunena. Pa zinthu zambiri m'moyo wa tsiku ndi tsiku monga kavalidwe, kakhalidwe komanso kayendetsedwe ka mpingo, munthu aliyense akuyenera kudziwa zoyenera kuchita ngakhale Baibulo silinena mwa mvemvemve. Munthu aliyense ali ndi mlingo wake wa zoyenera kuchita pa zinthu zimenezi koma osaweruza anthu omwe ali ndi maganizo osiyana ndi athu pa izi. Tiyeni tipitirize kukonda anthu omwe ali ndi maganizo osiyana nafe.

III. ZINDIKIRANI POMWE MAWU A PA NDIME NDI FANIZO CHABE

Mutenge ndime ya m'Baibulo kuti ndi fanizo pomwe Baibulo lanena kuti ndime-yo ndi fanizo. Nthawi zambiri Baibulo limanena kuti ndime-yi ndi fanizo kapena chining'a. Nthawi zina Baibulo limatha kuphatikiza zeni-zeni ndi fanizo m'ndime imodzi. Mawu ochokera pa Agalatiya 4 amati Phiri la Sinayi ndi chizindikiro cha ukaidi ndipo Yerusalemu ndi chizindikiro cha chisomo. Malo awiriwa alipodi pa dziko la pansu komanso ndi zizindikiro za choonadi cha uzimu.

Komanso muzitenga mawu ngati fanizo pomwe zinthu zomwe azitchula m'ndimeyo sizikugwirizana. Mwa chitsanzo, tengani ndime ngati fanizo pomwe chinthu chopanda moyo achigwiritsa ntchito ngati munthu kapena chinthu china cha moyo. M'malemba ochokera mu Uthenga wabwino wa Yohane, Yesu akumutchula ngati ndi chitseko, mkate komanso madzi. Mawu onsewa awagwiritsa ntchito ngati mafanizo.

Pa Afilipi 3 ndime ya 2, Paulo akuchenjeza: "Chenjerani ndi agalu" Apa Paulo akuchenjeza za gulu la anthu okhulupilira zokumva omwe amaphunzitsa kuti munthu opanda mdulidwe sangapulumsidwe. Choncho mu ndime imeneyi mawu oti galu ndi fanizo chabe. Pa Luka 13 ndime ya 32 Yesu akuti: "Pitani mukawuze nkhandwe-yo.." pomwe amakamba za Herod. Choncho mawu oti nkhandwe ndi fanizo mu ndime imeneyi.

Pali nthawi zina pomwe liwu limodzi amaligwiritsa ntchito ngati fanizo pa ndime zingapo koma ndi tanthauzo losiyana mu ndime zonsezo. Mwa chitsanzo, 'mkango' pa 1 Petulo 5 ndime ya 8 umatanthauza Satana koma 'mkango' pa Chivumbulutso 5 ndime ya 5 amanena Yesu. Choncho tanthauzo la mau aliwonse lizikhala mोगwirizana ndi m'mene liwu-lo aligwiritsira pa ndime imeneyo.

Dziwani kuti liwu silinganthuze zinthu ziwiri zosiyana pa nthawi imodzi. Ngati liwu aligwiritsa ntchito mu chiganizo ngati fanizo, limatenga tanthauzo la fanizo-lo. Ngati liwu aligwiritsa ntchito mwa tanthauzo lake leni-leni, liyenera kugwiritsidwa ntchito choncho.

IV. MUSATANTHAUZIRE MAU A MULUNGU M'NJIRA YANU

Musatanthuzire mau a Mulungu mogwirizana ndi kaganizidwe katsopano kapena nzeru za sayansi. Izi zimasintha ndi nthawi pomwe Baibulo ndi la muyaya ndipo silisintha. Kwa zaka zambiri, akatakwe a mbiri ya dziko akhala akunena kuti zomwe Baibulo limanena sizoona chifukwa palibe umboni oti mtundu wa chi-Hattussa (Hittite nation) omwe Baibulo limawutchula unakhalapodi pa dziko. Koma m'chaka cha 1907, akatswiri a mbiri anapeza miyala mdziko la Turkey yomwe imachitira umboni kuti mtundu-wu unalipodi.

Sikoyenera kupepesa pa zomwe Baibulo limanena koma sayansi ilibe umboni wake kapena kutanthuzira mau a Mulungu ndi cholinga choti agwirizane ndi umboni wa sayansi. Chifukwa Baibulo ndi mawu a Mulungu komanso choonadi cheni-cheni, chozizwitsa chilichonse komanso mfundo ina iliyonse imene Baibulo linena itengedwe kuti ndi choonadi.

V. MUSAUNAMIZIRE MZIMU OYERA

Pofuna kupeza choonadi cha mzimu oyera mu ndime iliyonse ya mau a Mulungu, anthu ambiri amayika mau mkamwa mwa mzimu oyera. Pamene munthu agwiritsa ntchito njira yolakwika pofuna kutanthauzira zinthu zoyenera, akuziyika yekha pa chiopsezo chonamizidwa ndi njira yakeyo.

Mwachitsanzo, pa Machitidwe 28, Paulo akukamba za m'mene anachiziridwa atalumidwa ndi njoka ya ululu ya mphiri. Munthu yemwe amayika mzimu mau mkamwa atha kunena kuti “Njoka yomwe ndi mdyerekezi, nthawi zonse imachitira chiwembu anthu olungama, koma imagonjetsedwa.

Kutanthauzira kwa mau a Mulungu uku mwina nkolondola pa ndime zina za Baibulo koma mawu ochokera pa Machitidwe 28 sakutiphunzitsa izi. Uku nkulakwitsa mawu a Mulungu.

TANTHAUZO LA

KUMVETSA	KUTANTHAUZIRA	KUCHITA ZOMWE TAPHUNZIRA
-----------------	----------------------	-------------------------------------

KODI NDICHITE CHANI?

- Zitsanzo za bwino ndi ziti?
- Tchimo lofuna kulisiya ndi liti?
- Zolakwitsa zofuna kuzipewa ndi ziti?
- Malonjenzo oyenera kuwakhulupilira ndi ati?
- Malamulo oyenera kuwatsatira ndi ati?
- Zoyenera kuchita ndi chain?

NDONDOMEKO YOPHUNZIRIRA MALEMBA A M’BAIBULO

MITUNDU	MITUNDU YA NKHANI (KUFOTOKOZA)	NKHANI ZOPHUNZITSA (MAKALATA)	NKHANI ZOLEMBEDWA M’NDAKATULO, MAFANIZO, ZOLOSERA KOMANSO ZOVUMBULUTSA
CHITSANZO	<ul style="list-style-type: none"> Mbiri (Kukamba m’mene zinthu zinachitikira) <p>Zitsanzo:</p> <ul style="list-style-type: none"> Mauthenga abwino monga- Machitidwe, Ekisodo, Levitiko, Numeri ndi mabuku ena komanso nkhani zina za Chipangano chakale monga bukhu la Mafumu. 	<p>Kufotokoza nkhani mwatsatanetsatane</p> <p>Makalata a Paul kwa-Agalatiya, Aroma, Tito ndi ena ambiri</p> <p>Zolembe za Petulo, Yohane, Yakobo komanso ziphunzitso za Yesu</p>	<p>Kulemba mfundo mundondomeko zosiyanasiyana. Amagwiritsa ntchito mafanizo pofuna kufotokoza mfundo.</p> <p>Izi ndi monga: Masalimo, Nyimbo ya Solomo, Yesaya, Yeremiya komanso ma mafanizo osiyanasiyana amene Yesu amagwiritsa ntchito pophunzitsa.</p>
ZIZINDIKIRO ZIKULU-ZIKULU ZA MTUNDU	Anthu, malo, zochitika komanso umunthu.	Mfundo, mawu, ziganizo, ndime	Mungazindikire ndime izi powona miyambi, mafanizo ndi zina zotero.

NDONDOMEKO YOPHUNZIRIRA MALEMBA A M’BAIBULO

MITUNDU	MITUNDU YA NKHANI (KUFOTOKOZA)	NKHANI ZOPHUNZITSA (MAKALATA)	NKHANI ZOLEMBEDWA M’NDAKATULO, MAFANIZO, ZOLOSERA KOMANSO ZOVUMBULUTSA
<p>ZOMWE</p> <p>ZINGAKUTHANDIZENI</p> <p>KUMVETSA</p> <p>MALEMBA</p>	<p>Zifunseni:</p> <ul style="list-style-type: none"> • Nkhani ikukhudza ndani? • Ndime ikuti chiyani? • Zinachitika liti? • Zinachitikira kuti? • Zinachitika bwanji? <p>Fotokozaninso nkhaniyo</p> <p>Yang’anani kuti mbali zosiyanasiyana zomwe zikukambidwa mu nkhaniyo zikugwirizana bwanji?</p> <p>Yesani kumva m’mene anthu akukambidwa mu nkhani-mo amamvera pomwe nkhaniyo imachitika</p> <p>Zitengeni inu ngati muli mu nkhaniyo.</p> <p>Mukuwona chain? Mukumva bwanji? Mukuganiza chain?</p>	<p>Fotokozani mwatsatanetsatane m’mene mfundo zikulu-zikulu azifotokozera m’ndimeyo</p> <p>Lembani mawu omwe awabwereza</p> <p>Yang’anani zinthu izi:</p> <ul style="list-style-type: none"> • Kufananiza zinthu • Kusiyanyitsa zinthu • Mawu olumikiza monga: <ul style="list-style-type: none"> ✓ Choncho ✓ Kotero kuti ✓ Chifukwa ✓ Kwa ✓ Kuchokera <p>Lemba lililonse limathandiza kumvetisa ndime yonse</p>	<p>Alakatuli a chi-Heberi amakonda kulemba ziganizo za nthira-kuwiri. Mfundo imodzi inali ndi matanthauzo awiri.</p> <p><i>Mwambi ndi chiganizo chomwe makhalidwe a anthu amawafanizira ndi zinthu za chilengedwe.</i></p> <p>Chitsanzo Miyambo 5 ndime ya 3</p> <p>Fanizo ndi luso lapadera lomwe Yesu anali nalo lomabisira choonadi kwa iwo omwe samafuna kumva chowonadi.</p> <p>Kulosera ndi chivumbulutso ndi kuthekera konena za mtsogolo motsogozedwa ndi mphamvu ya mzimu oyera.</p>

NDONDOMEKO YOPHUNZIRIRA MALEMBA A M'BAIBULO

<p>ZOMWE</p> <p>ZINGAKUTHANDIZENI</p> <p>KUTANTHAUZIRA</p> <p>MALEMBA</p>	<p>ZOTHANDIZIRA KUTANTHAUZIRA MALEMBA NDI ZOFANA PA MITUNDU YONSE YA KALEMBEDWE KA MALEMBA</p> <p>Iyi ndi njira yofuna kudziwa kuti anthu omwe amva mawu koyamba awatanthauzira bwanji.</p> <ol style="list-style-type: none">1. Kodi mlembi amafuna kutanthauza chiyani polemba m'njira imeneyi?<ul style="list-style-type: none">❖ Penyani❖ Imvani m'nthupi mwanu❖ Ganizani2. Ndi chifukwa chain mlembi walembe izi?3. Kodi anthu omwe analipo pa nthawi yomwe amalembe Baibulo akanatanthauzira bwanji malemba-wa? <p>Pali zina zomwe zingathandize kwambiri kumvetsa mawu ochokera m'malembe omwe cholinga chawo ndikuphunzitsa.</p> <ol style="list-style-type: none">a) Kodi mfundo imeneyi yabwera chifukwa chain?b) Kodi mlembi analemberanji mfundo imeneyi?c) Kodi mlembi akanatha kugwiritsa ntchito mawu ena polemba mfundo imeneyi?d) Kodi mfundo-yi ikutanthauza chain?e) Kodi mfundo imeneyi ikugwirizana bwanji ndi zomwe zinachitika mfundo yotsatira isanabwere?f) Kumvetsa zinthu m'chimake nkofunika kwambiri
---	--

NDONDOMEKO YOPHUNZIRIRA MALEMBA A M'BAIBULO

<p>ZOMWE ZINGAKUTHANDIZENI</p> <p>KUCHITA ZOMWE TAPHUNZIRA</p> <p>MALEMBA</p>	<p>ZOTHANDIZIRA KUGWIRITSA NTCHITO ZOMWE TAPHUNZIRA NDI ZOFANA PA MITUNDU YONSE YA KALEMBEDWE KA MALEMBA</p> <ol style="list-style-type: none">1. Pemphani Mzimu Woyera kuti ukuphunzitseni kugwiritsa ntchito zomwe mwaphunzira 1 Akorinto 2 ndime ya 9 mpaka 162. Wunikirani zomwe mwaphunzira ku moyo wanu monga wa tsiku ndi tsiku: Kodi pali chitsanzo chomwe tingatsatire? Kodi pali tchimo lomwe tingalisiye? Kodi pali zolakwitsa zomwe tingazipewe? Kodi pali lonjezo lomwe tingafune kukwaniritsidwa? Kodi pali lamulo lomwe tikuyenera kutsatira?3. Tinene kuti chain tsopano Kodi ndakonza kuti ndichitapo chiyani? Kodi zimenezi zisintha chiyani pa moyo wanga? Kodi ndi ndondomeko yanji yomwe ndikonze pa moyo wanga? Ndipanga chani? Ndikwaniritsa bwanji?
---	---

Zoti muchite

NDIME YOLONGOSOLA

Ntchito yoyamba

M’Baibulo muli mabuku ambiri omwe amalongosola nkhani kapena mbiri. Nkhanizi ndizosavuta kumvetsa. M’chipangano chakale, mabuku omwe amafotokoza nkhani ndi monga mabuku a malamulo a Mose kuyambira Genesis mpaka Detoronomo komanso mabuku olongosola mbiri kuyambira Yoswa mpaka Estere. M’chipangano chatsopano mabuku olongosola nkhani ndi monga mauthenga abwino komanso machitidwe.

Ntchito yoyambayi muyankha mafunso osiyanasiyana pa ndime zomwe tikupatseni. Mafunsowa cholinga chake ndikuwunikira m’mene mungafunsire mafunso ogwirizana ndi nthambi zitatu zomwe tikukambirana m’bukhulu. Nthambi-zi ndi kumvesetsa malemba, kutanthauzira malemba ndi kugwiritsa ntchito zomwe taphunzira m’malemba. Kutsogoloku, mudzayesera kupanga mafunso otere pa inu nokha.

1. Werengani malemba omwe ali pa Mariko 2 ndime 1 mpaka 12 kangapo. Yesetsani kuwamvesetsa mawu-wa bwino lomwe.
2. Yankhani mafunso omwe ali pa tsamba lotsatira. Yesetsani kumaliza ntchito-yi. Musataye nthawi yanu pa funso limodzi.

MARKO 2 NDIME 1 MPAKA 12

1. Ndipo polowanso Iye m'Kapernaο atapita masiku ena, kunamveka kuti ali m'nyumba.
2. Ndipo ambiri anaunjikana, kotero kuti anasowa malo ngakhale pakhomo pomwe: ndipo analankhula nawo mau.
3. Ndipo anadza kwa Iye otenga munthu wodwala manjenje, wonyamulidwa ndi anthu anai.
4. Ndipo pamene sanakhoza kufika kuli Iye, chifukwa cha khamu la anthu, anasasula chindwi pokhala iye; ndipo pamene anatha kuliboola, anatsitsa mphasa m'mene alikugonano wodwala manjenjeyo.
5. Ndipo Yesu pakuwona chikhulupiliro chawo, ananena ndi wodwala manjenje, Mwana, machimo ako akhululukiridwa.
6. Koma anakhalapo ena alembi akuganizira mumtima mwawo,
7. Munthu amene atero bwanji? Achita mwano; akhoza ndani kukhululukira machimo koma m'modzi ndiye Mulungu?
8. Ndipo pomwepo Yesu pozindikira mumtima mwake kuti alikuganiza chomwecho mwa iwo okha, ananena nawo, muganiza bwanji zinthu izi m'mitima yanu?
9. Chapafupi nchiti, kapena kuuza wodwala manjenje kuti, Machimo ako akhululukidwa; kapena kuti, Nyamuka, senza mphasa yako nuyende?
10. Koma kuti mudziwe kuti Mwana wa munthu ali mwini ulamuliro wakukhululukira machimo pa dziko lapansi (ananena ndi wodwala manjenje),
11. Ndikuuza iwe, Nyamuka, senza mphasa yako, numuke kwanu.
12. Ndipo ananyamuka iye pomwepo, nasenza mphasa, naturuka pamaso pa iwo onse; kotero kuti anadabwa onse, nalemekeza Mulungu, nanena kuti, Zotere sitinazione ndi kale lonse.

Ntchito voyamba

Mafunso ochokera pa Mariko 2 ndime 1 mpaka 12

1. Anthu omwe atchulidwa mu nkhaniyi ndi ndani? (Funso loyesa kumvesetsa)

2. Mu nkhaniyi, kodi Yesu anali kuti? (Funso loyesa kumvesetsa)

3. Kodi chinachitika ndi chani mu nkhaniyi? Longosolaninso nkhaniyi m'mene mukuyimvetsera (Funso loyesa kumvesetsa)

4. Kodi mavuto ena amene munthu wodwala manjenje amakomana nawo ndi otani? (Funso loyesa kutanthauzira)

5. Kodi ndi kovuta bwanji kuti munthu wodwala manjenjeyu afike kwa Yesu? (Funso loyesa kumvesetsa).

- 6a. Kodi amuna anayi-wa anali otani? (Funso loyesa kutanthauzira)

Ntchito yoyamba

6b. Chifukwa chani amakakamira? (Funso loyesa kutanthauzira)

6c. Kodi Yesu amakamba za chikhulupiliro cha ndani pa nthawi imeneyi? (Funso loyesa kutanthauzira)

7. Ndi chifukwa chiyani Yesu ananena kuti: “Mwana, machimo ako akhululukiridwa.”? (Funso loyesa kutanthauzira)

8. Kodi alembi akutsutsa chiyani pa zoyankhula za Yesu? (Funso loyesa kutanthauzira)

9. Yesu anayamba kuyankha mafunso awo nthawi iti? (Funso loyesa kutanthauzira)

10. Werenganinso ndime 9 mpaka 10 ya malembawa. Kodi chosavuta kufotokoza ndi chani? Chifukwa chani? (Funso loyesa kutanthauzira)

11. Kodi tchimo ndi kudwala manjenje zimagwirizana bwanji? (Funso loyesa kutanthauzira).

12. Munthu odwala manjenje ali ngati chiyani? (Funso loyesa kutanthauzira)

13. Kodi Khristu amawapangira chiyani anthu ochimwa? (Funso loyesa kutanthauzira)

Ntchito yoyamba

14. Kodi mfundo yaikulu pa malemba-wa ndi iti? (Funso loyesa kutanthauzira)

15. Kodi muli ndi chikhulupiro chotengera munthu odwala manjenje mu uzimu kwa Khristu? (Funso loyesa kuchita zomwe taphunzira)

Lembani ndondomeko za m'mene mungachitire

16. Lembani zopsinja zomwe munakomana nazo pobweretsa anthu kwa Khristu. (Funso loyesa kuchita zomwe taphunzira).

Zipsinjo zimene-zi mungathane nazo bwanji?

17. Lembani njira zotheke zomwe mungapange pofuna kuwonetsa kuti mumasamalira anthu ochimwa? (Funso loyesa kuchita zomwe taphunzira)

18. Kodi mungagwire bwanji ndi anthu ena pofuna kubweretsa anthu kwa Khristu? (Funso loyesa kuchita zomwe taphunzira).

**NDINU MTUMIKI OPITA KWA ANTHU
KUMBUKIRANI KUTI TCHIMO LIMAZIZIRISA ZIWALO!**

Ndakatulo

Ndakatulo za chi-Heberi mumakhala miyambi ndi zining'a zambiri. Ndakatulo-zi zimapereka uthenga pojambula zithunzi mogwiritsa ntchito mawu kwa awerengi.

Chomwe chimapangitsa ndakatulo za chi Heberi kukhala zosiyanana ndi zina ndi kulumikizana kwa mfundo za ziganizo zotsatirana kapena ndime zotsatirana. Kubwerezabwereza kwa mfundo kumathandiza kuwonetsa zomwe mlembi wa ndakatulo amafuna kutanthauza. Mu ntchito yakutsogoloku muzawona kufunika kwa izi.

Mu ntchito ino, muwerenga ndime yosavuta ya ndakatulo. Koma poyamba muphonzira njira ziwiri zofunikira kwambiri m'bukhu lino pophonzira ndi kumvesetsa malemba. Njirazi ndi kudulira ndime ndi kuwerenganso ndime mwadulirayo mozama.

NJIRA YOPHUNZIRIRA MALEMBA A M'BAIBULO

KUDULIRA NDIME

Mfundo yaikulu

Kuduladula kalata

Kuduladula mitundu ina ya malemba

KUWERENGANSO MALEMBA MOZAMA

Mfundo yaikulu

Chitsanzo cha kuwerenganso malemba mozama

I. KUDULIRA NDIME

Cholinga chodulira ndime ndikufuna kuyamba kuyimvetsa ndime-yo mozama. Pali njira zambiri zodulira ndime. Cholinga ndi kuduladula ndime-yo m'zidutswa malinga ndi mfundo zomwe zili m'ndime-yo. Muyenera kusanthula mfundo ina iliyonse yomwe ili m'ndimeyo ndi cholinga choyimvesetsa bwino. M'maphunziro anu tikuphunzitsa njira ziwiri zodulira ndime.

- A. Njira yosavuta yodulira ndime yomwe ingagwiritsidwe ntchito pa bukhu lina lililonse la m'Baibulo.
- B. Njira yodulira ndime m'makalata a m'Baibulo yomwe imapangitsa kuphunzira malemba a m'makalata-wa mosavuta.

A. NJIRA YOSAVUTA YODULIRA NDIME MALEMBA

Njirayi mutha kuyigwiritsa ntchito pofuna kumvetsa mozama malemba a m'bukhu lina lililonse la m'Baibulo. Pogwiritsa ntchito njira-yi, mumangowerenga ndime ya malemba ndikusanthula mfundo zomwe zili m'malemba-mo, nkumawonesetsa pomwe mfundo yayambira ndikuthera.

Poyamba werengani ndime mozama kangapo. Kenaka yambani kusanthula mfundo zikulu-zikulu mu ndime-yo. Pezani mfundo yaikulu imodzi yomwe ndime-yo ikukamba. Zinthu ziwiri zofunika kwambiri kuchita pamene mukugwiritsa ntchito njira-yi nazi:

CHOYAMBA: Lembani mfundo yaikulu yomwe ndime ikulongosola

CHACHIWIRI: Lembani mfundo zonse zomwe zili mu malemba ndi ndime yomwe mfundoyo tatuluka.

NTHAWI ZONSE PANGANI IZI MWATSATANETSATANE KUCHOKERA NDIME INA KUFIKA NDIME YOTSATIRA

ZITSANZO ZOSAVUTA ZA NJIRA YODULIRA NDIME

MASALIMO 128

MFUNDO YAIKULU: *Nkwabwino kuopa Yehova*

- I. Zipatso zoopa Yehova (Ndime 1 mpaka 4)
- II. Zotsatira za chimwemwe (Ndime 5 mpaka 6)

EZARA

MFUNDO YAIKULU: *Kumanganso kachisi*

- I. Kumanganso kachisi ndi Zurubabele (Ezara 1 mpaka 6)
 - A. Kubwerera koyamba kwa Ayuda (Ezara 1 mpaka 2)
 - B. Kumanganso kachisi (Ezara 3 mpaka 6)
- II. Kusintha kwa zinthu pansi pa ulamuliro wa Ezara (Ezara 7 mpaka 10)
 - A. Kubwerera kwachiwiri kwa Ayuda (Ezara 7 ndime 1 mpaka 8)
 - B. Kusintha kwa anthu (Ezara 8 ndime 33, Ezara 10 ndime 44)

B. KUDULIRA KALATA: Makalata ambiri a m’Baibulo amalembedwa mwa tsatanetsatane monga kalata ina iliyonse (Kupatula makalato omwe apezeka ku Aheberi ndi 1 Yohane). Mukamawerenga kalata, wonesetsani mau oyamba a kalatayo-moni omwe mlembi amapereka kwa omwe akuwalemba kalata. Nthawi zambiri akatha malonje-wa mlembi amathokoza. Kenaka amanena cholinga cha kalata-yo kuchoka apo amalemba chiphunzitso chachikulu chimene walemba kalata-yo ndipo pomaliza amalawira.

1. MAU OYAMBA

Ndime zochepa zoyamba ndi malonje. Pambuyo pa malonje nthawi zambiri pamabwera kuthokoza.

2. CHOLINGA CHA KALATA

(Cholinga cholemba kalata-yi ndi chiyani?) Muzapeza cholinga cha kalata m’ndime zosaposa zitatu. Mlembi amafotokoza cholinga cha kalata mosatalikitsa nkhani ndipo amafotokoza izi pambuyo pa malonje ndi kuthokoza. Yang’anani mozama kuti mupeze cholinga cha kalata chifukwa ndiye khomo la kalata-yo.

3. PHUNZIRO LALIKULU

Ntsanamira ya kalata yagona pamenepa. Mfundo zosiyanasiyana amazikamba m’ndime zingapo. Nthawi zina mfundo amangozikamba m’ndime zochepa koma nthawi zina amazikamba m’ndime zochuluka. Kumbukirani kuti ndime za m’Baibulo sizimagwirizana ndi kuchuluka kwa mfundo zomwe azifotokoza. Yang’anani mozama mfundo m’ndime-zo. Mwachitsanzo, m’kalata nkutheka kuti ndime 5 mpaka 10 ikukamba za chikondi pomwe ndime 11 mpaka 16 ikukamba za chigamulo kapena chisangalalo.

4. MAWU OMALIZA

Kalata amayimaliza ndi mfundo zomaliza kapena mawu otsendera. Nthawi zina mawu-wa timawagwiritsa ntchito m’chalichi ngati m’dalitso.

CHITSANZO CHA KUDULIRA KALATA

BUKHU LA TITO

MAWU OYAMBA

Tito 1 ndime 1 mpaka 4

Gawo loyamba: Tito 1 ndime 1 mpaka 4

Malonje

Gawo lachiwiri

Kuthokoza

VI. CHOLINGA CHA KALATA Tito 1 ndime 5

Zolinga ziwiri:
Kukhazikitsa
mpingo
ndikusankha akulu a
mpingo

VII. CHIPHUNZITSO CHACHIKULU M'KALATA

Tito 1 ndime 6 komanso Tito 3 ndime 16

Kusankha
Atsogoleri a
mpingo
komanso
kukhazikitsa
mpingo

Mfundo zitatu zikulu-zikulu

Gawo loyamba: Tito 1 ndime 6 mpaka 16: Zoyeneretsa atsogoleri kugwira
ntchito ya mpingo

Gawo lachiwiri: Tito 2 ndime 1

Komanso Tito 3 ndime ya 11: Chiphunzitso chabwino komanso udindo wa
akhiristu mu mpingo

Gawo lachitatu: Za ku mtima kwa mlembi

VIII. MAWU OMALIZA

Tito 3 ndime 15

II. KUWERENGANSO MOZAMA NDIME YOMWE MWADULIRA

Ngati mwamaliza kudulira ndime ndi inu okonzeka tsopano kuyamba kumvesetsa malemba mozama. Mungakwaniritse izi pomvesetsetsa malemba, kuwathanthauzira moyenera komanso kuchita zomwe taphunzira pa malemba. Werenganinso ndime zomwe mwadulira iliyonse payokha mozama kumvesetsa tanthauzo la liwu liri lonse, ziganizo komanso mfundo zonse zomwe zili mu ndime.

(Chitsanzo chotsatira chikukuwonetsani m'mene njirayi amayigwiritsira ntchito)

AFILUPI 1 ndime 1 mpaka 6 **Chitsanzo cha kawerengedwe mozama ka ndime yomwe mwayidulira**

Kumvesetsa malemba (Kutha kulongosola mfundo zikulu-zikulu zomwe malemba akufotokoza)	Kutanthauzira malemba (Kutha kufotokoza zomwe malemba akutanthauza)	Kuchita zomwe malemba akuphunzitsa (Kulongosola m'mene tingagwiritsire ntchito m'moyo wa tsiku ndi tsiku zomwe malemba akuphunzitsa)
<p>1. Mfundo yochokera pa ndime 1 mpaka 2</p> <p>Pa ndime iyi tipeza mawu oyamba a m'bukhuli.</p> <p>Ndime 1 akukamba za Paulo ndi Timoteo</p> <p>Akukambanso za kapolo wa Yesu Khristu</p>	<p>Pafupi-fupi makalata onse ali ndi mawu oyamba</p> <p>Paulo ndiye mlembi wa malemba awa koma watchulamonso dzina la Timoteo.</p> <p>Paulo akuzindikira kuti ali ndi moyo ndi cholinga chotumikira Yesu.</p>	<div style="border: 1px solid black; padding: 5px; margin-bottom: 10px;"> <p>DZIWANI KUTI: Pamene mwazindikira m'mene mungagwiritsire ntchito zomwe mwaphunzira ndiye kuti mukuchita zomwe malemba akuphunzitsa</p> <p>KODI MUPANGA CHIYANI? MUPANGA MOTANI?</p> </div> <p>Ndikufuna kukhala kapolo wa Yesu. M'njira yanji?</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Pokhala ndi mtima ngati wakapolo wa Yesu 2. Kuphunzitsa Sunday School 3. Kugwira ntchito mu mpingo mozipereka
<p>Kwa oyera mwa Yesu Khristu</p> <p>Ndime 2: Chisomo ndi Mtendere wa kwa Mulungu</p>	<p>Paulo akulemba kwa anthu okhulupilira. Munthu oyera si chosema koma munthu obadwanso mwatsopano.</p> <p>Mawu amene Paulo amagwiritsa ntchito nthawi zambiri popereka malonje m'makalata ake.</p> <p>Chisomo-Kukonderedwa ndi Mulungu Mtendere: Kukhala opanda mantha ndi nkhwana m'mitima yathu.</p>	<p>Ine ndi oyera mtima chifukwa cha Yesu m'moyo mwanga. Choncho ndizakhala moyo olungama monga Yesu anachitira.</p> <p>Ndili ndi Chisomo ndi Mtendere zochokera kwa Mulungu mu mtima mwanga. Choncho sindiyenera kukhala wa mantha. Moyo wanga umayendetsedwa ndi Chisomo ndi Mtendere Wake.</p>
<p>2. Mfundo yochokera pa ndime 3 mpaka 6</p> <p>M'ndime imeneyi tipezamo cholinga cha kalatayi</p> <p>Ndime 4: Pembedzo ndi kukondwera</p>	<p><i>Paulo ali ndi chisangalalo osati chifukwa cha moyo wake koma chifukwa cha ntchito za Yesu Khristu m'moyo mwake.</i></p>	<p>Ngakhale nditakomana ndi zovuta za mtundu wanji, nditha kukhala okondwera chifukwa cha ntchito za Yesu m'moyo mwanga</p>

Ndakatulo Ntchito yachiwiri

- 1. Werengani mawu ochokera pa Masalmo 1 kangapo.**
- 2. Dulirani mawu-wo pogwiritsa ntchito njira yodulira malemba yosavuta yomwe mwaphunzira m’bukhu lino**
- 3. Werengani mozama malemba a pa ndime yomwe mwadulirayo.**

MASALMO 1

1. WODALA munthuyo osayenda mu uphungu wa oipa, Kapena wosayimilira m’njira ya ochimwa, Kapena wosakhala pansu pa bwalo la onyoza.
2. Komatu m’chilamuliro cha Yehova muli chikondwerero chake; Ndipo m’chilamuliro chake amalingilira usana ndi usiku.
3. Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi; Wakupatsa chipatso chake pa nyengo yake, Tsamba lake lomwe losafota; Ndipo zonse azichita apindula nazo.
4. Oyipa satero ayi; Koma akunga mungu owuluka ndi mphepo.
5. Chifukwa chake oyipa sadzayimirira pa mlandu-wo, Kapena ochimwa mu msonkhano wa olungama.
6. Pakuti Yehova adziwa mayendedwe a olungama; Koma mayendedwe a oyipa adzatayika.

I. MFUNDO YAIKULU _____

II. DULIRANI NDIME: (Lembani mfundo)

1. Ndime _____

2. Ndime _____

3. Ndime _____

III. WERENGANI MOZAMA NDIME YOMWE
MWADULIRA:

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

Kalata

Ntchito yachitatu

Pano muphunzira malemba a m'kalata pogwiritsa ntchito njira yodulira ndime komanso kuwerenga ndime yomwe mwadulira-wo mozama. Werenganinso m'mene mungapangire izi kuchokera pa tsamba 28 kufikira tsamba 34.

- 1. Werengani mawu ochokera pa Yuda 1 ndime 1 mpaka 25 kangapo.**
- 2. Dulirani mawu-wo pogwiritsa ntchito njira yodulira malemba a m'kalata yomwe mwaphunzira m'bukhu lino pa tsamba 31**
- 3. Werengani mozama malemba a pa ndime yomwe mwadulirayo kutsatira chitsanzo chomwe chili pa tsamba 34 la bukhu lino.**

YUDA

1. Yuda, kapolo wa Yesu Khristu, ndi m'bale wake wa Yakobo, kwa iwo oitanidwa, okonedwa mwa Mulungu Atate, ndi osungidwa ndi Yesu Khristu :
2. Chifundo ndi mtendere ndi chikondi zikuchulukireni.
3. Okonedwa, pakuchita changu chonse chakukulemberani za chipulumutso cha ife tonse, ndafulumidwa mtima ine kukulemberani ndi kudandaula kuti mulimbanetu chifukwa cha chikhulupiro chapatsidwa kamodzi kwa ojera mtima.
4. Pakuti pali anthu ena anakwawira mtseri ndiwo amene aja adalembedwa maina awo kale kukalandira chitsutso ichi, anthu osapembedza, akusandutsa chisomo cha Mulungu wathu chikhale chilakolako chonyansa, nakaniza Mfumu wayekha, ndi ambuye wathu Yesu Khristu.
5. Koma ndifuna kukukumbutsani mungakhale munadziwa zones kale kuti Ambuye, atapulumutsa mtundu wa anthu ndi kuwaturutsa m'dziko la Aigupto, anawononganso iwo osakhulupirira.
6. Angelonso amene sanasunga chikhaldwe chawo choyamba, komatu anasiya pokhala pawo pawo, anawasunga m'ndende zosatha pansa pa mdima, kufikira chiweruzo cha tsiku lalikuru.
7. Monga Sodoma ndi Gomora, ndi midzi yakuizungulira, potsatana nayoyo, idazipereka kudama, ndikutsata zilakolako zachilendo, iyikidwa chitsanzo, pakuchitidwa chilango cha moto wosatha.
8. Momwemonso iwo m'kulota kwawo adetsa matupi awo, napepusa ufumu, nachitira mwano maulemerero.
9. Koma Mikayeli mkulu wa angelo, pakuchita makani ndi mdierekezi anatsutsana za thupi la Mose, sanalimbika mtima kumchulira chifukwa chomchitira mwano, koma anati, Ambuye akudzudzule.
10. Koma iwowa zimene sazidziwa azichitira mwano; ndipo zimene azizindikira chibadwire, monga za moyo zopanda nzeru, mu izi atayika.
11. Tsoka kwa iwo! Pakuti anayenda m'njira ya Kaini, ndipo anadziwononga m'chisokero cha Balamu. chifukwa cha kulipira, natayika m'chitsutsano cha Kore.
12. Iwo ndiwo okhala mawanga mawanga pa mapwando anu a chikondano, pakudya nanu pamodzi, akudziweta okha opanda mantha; mitambo yopanda madzi, yotengekatengeka ndi mphepo; mitengo ya masika yopanda zipatso; yofafa kawiri, yozuka mizu

13. Mafunde owopsa a nyanja, akuwinduka thovu la manyazi a iwo okha; nyenyezi zosokera, zimene mdima wakuda bii, udazisungikira kosatha.
14. Ndipo kwa iwo, Henoke wachisanu ndi chiwiri kuyambira kwa Adamu, ananenera kuti, Tawona wadza ambuye ndi oyera ake zikwi makumi,
15. Kudzachitira onse chiweruzo, ndikusutsa osapembedza onse, pa ntchito zawo zonse zosapembedza, zimene anazichita kosapembedza, ndi pa zolimba zimene ochima osapembedza anayankhula pa Iye.
16. Amenewo ndiwo odandaula, oderera, akuyenda monga mwa zilakolako zawo (ndipo pakamwa pawo akalankhula zazikuruzikuru), akutama anthu chifukwa cha kupindula nako.
17. Koma inu abale, mukumbukire mawu onenedwa kale ndi atumwi a Ambuye wathu Yesu Khristu;
18. Kuti ananena nanu, Pa nthawi yotsiriza padzakhala otonza, akuyenda monga mwa zilakolako zosapembedza za iwo okha.
19. Iwo ndiwo opatukitsa, anthu a makhalidwe achibadwidwe, osakhala naye Mzimu.
20. Koma inu, okonedwa, podzimangirira nokha pa chikhulupiliro chanu
21. Choyeretsa ndikupemphera mu Mzimu Woyera,
22. Mudzisunge nokha m'chikondi cha Mulungu, ndikulindilira chifundo cha Ambuye wathu Yesu Khristu, kufikira moyo wosatha.
23. Ndipo ena osinkhasinkha muwachitire chifundo,
24. Koma ena muwapulumutse ndi kuwakwatula ku moto; koma ena muwachitire chifundo ndi mantha, nimudane nawonso maraya ochitidwa mawanga ndi thupi.
25. Ndipo kwa Iye amene akhoza kukudikirani mungakhumudwe, ndi kukuimikani pamaso pa ulemerero wache opanda chilema n'kukondwera,
26. Kwa Mulungu wayekha, Mpulumutsi wathu, mwa Yesu Khristu Ambuye wathu, zikhale ulemerero, ukulu, mphamvu, ndi ulamuliro zisanayambe nthawi, ndi tsopano, ndikufikira nthawi zones. Amen.

I. DULIRANI NDIME:

A. Mawu Oyamba Ndime: _____

B. Cholinga cha kalata Ndime: _____

C. Phunziro lalikulu Ndime: _____

 Phunziro loyamba: _____ Ndime: _____

 Phunziro lachiwiwi: _____ Ndime: _____

D. Mawu Otsiriza Ndime: _____

**II. KUWERENGA MOZAMA NDIME YOMWE
MWADULIRA
KUPHUNZIRA MALEMBA OCHOKERA PA YUDA**

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

Ndakatulo za chi-Heberi

Ntchito yachinayi

- 1. Werengani mawu ochokera pa Masalmo 139 kangapo.**
- 2. Dulirani mawu-wo pogwiritsa ntchito njira yodulira malemba yosavuta yomwe mwaphunzira m’bukhu lino**
- 3. Werengani mozama malemba a pa ndime yomwe mwadulirayo**
- 4. Zindikirani kuti kodi ndakatulo-yi ikugwiritsa mitundu ingati yakabwerezedwe ka mawu.**

Ndakatululo za chi-Heberi

I. MLOZERA: GWIRITSANI NTCHITO KABWEREZEDWE KA MAWU M'NDAKATULO ZA CHI- HEBERI POPEZA TANTHAUZO LA NDIME

- A. M'ndakatulu mumakhala zining'a zambiri choncho tiyenera kuphunzira kutanthauzira mawu omwe sakutanthauza zinthu za tsiku ndi tsiku. Tithe kuwona chithunzithunzi chomwe mawu a m'ndakatulo akufuna kutiwonetsa.
- B. Chinthu chosasowa mu ndakatulo za chi-Heberi ndikubwerezabwereza mfundo m' ziganizo zotsatirana kapena ndime zotsatirana.
- C. Ndakatulo za chi-Heberi amabwerezabwereza mfundo. Izi zimathandiza kumvesetsa tanthauzo lake.

II. PALI KABWEREZEDWE KA MFUNDO KA MITUNDU ITATU M'NDAKATULO ZA CHI-HEBERI

- A. KUBWEREZA MFUNDO MOFANANA-Mfundo amayitchula kachiwiri kapena kachitatu m'mene anayitchulira koyamba.

CHITSANZO: “Tamvani mau anga Ada ndi Zila; Inu akazi a Lameke, mverani kunena kwanga!” (Genesis 4 ndime 23).

“Mubwereze kunditsuka mphulupulu yanga, ndipo mundiyeretse kundichotsera choipa changa.” (Masalmo 51 ndime 2).

- B. KUBWEREZA MFUNDO MOWONJEZERA-Mlakatuli amawonjezera pa mfundo yoyamba

CHITSANZO: Masalmo 1 ndime 1. Gawo lowonjezera m'chiganizo chilichonse limawonjezera mfundo yatsopano ku mfundo yoyamba. “Wodala munthuyo wosayenda mu uphungu wa oyipa, Kapena wosaimilira m'njira za ochimwa, Kapena wosakhala pansu pa bwalo la onyoza.

- C. KUBWEREZA MFUNDO MOTSUTSA-Mlakatuli amalemba mfundo zotsutsana.

CHITSANZO: “Lilime la anzeru linena bwino zomwe adziwa; Koma m'kamwa mwa opusa mutsanulira utsiru.” (Miyambo 15 ndime 2).
Gawo lachiwiri la chiganizo likutchula zinthu zotsutsana ndi zomwe gawo loyamba lanena.

Ntchito yachinayi

MASALMO 139

1. Munandisanthula Yehova, nimundidziwa.
2. Inu mudziwa kukhala kwanga ndikuuka kwana, Muzindikira lingaliro langa muli kutali.
3. Muyesa popita ine ndi pogona ine, ndi njira zanga zonse muzolowerana nazo.
4. Pakuti asanafike mawu pa lilime langa, tawonani, Yehova, muwadziwa onse.
5. Munandizinga kumbuyo ndi kumaso, nimunaika dzanja lanu pa ine.
6. Kudziwa ichi kundilaka ndi kundidabwitsa: Kundikhalira patali, sindifikirako.
7. Ndidzapita kuti kuzembera mzimu wanu? Kapena ndidzathawira kuti kuzembera nkhope yanu?
8. Ndikakwera kumka kumwamba, muli komweko; kapena ndikadziyalira ku Gehena, tawonani muli komweko.
9. Ndikadzitengera mapiko a mbanda kucha, ndikukhala ku malekezero a nyanja;
10. Kungakhale komweko dzanja lanu lidzanditsogolera, nilidzandigwira dzanja lanu la manja.
11. Ndipo ndikati, koma mdima undiphimbe, ndi kuunika kondizinga kukhale usiku;
12. Ungakhale mdima sudetsa pamaso panu, koma usiku uwala ngati usana: mdima ukuunga ngati kuwunika.
13. Pakuti ino munalenga imso zanga; munandiumba ndisanabadwe ine.
14. Ndikuyamikani chifukwa kuti chipangidwe changa nchoopsa ndi chodabwitsa; ntchito zanu nzodabwitsa; moyo wanga uchidziwa ichi bwino ndithu.
15. Thupi langa silinabisikira Inu popangidwa ine mobisika, poumbedwa ine monga m'munsi mwake mwa dziko lapansi.
16. Ndisanaumbidwe ine maso anu anandipenya, ziwalo zanga zonse zinalembedwa m'bukhu mwanu, masiku oti ziumbidwe, pakalibe chimodzi cha izo.

17. Potero, Mulungu, ndiziyesa zolingalira zanu za mtengo wache ndithu!
Mawerengedwe ache ndi ambirimbiri!
18. Ndikaziwerenga zichuluka kuposa mchenga: ndikauka ndikhalanso nanu.
19. Indedi, mudzaomba woipa, Mulungu: ndipo amuna inu okhumba mwazi chokani, kwa ine.
20. Popeza anena za Inu moipa, ndi adani anu achula dzina lanu mwachabe.
21. Kodi sindidana nawo iwo akudana ndi Inu Yehova? Ndipo kodi sindimva nawo chisoni iwo akuwukira Inu?
22. Ndidana nawo ndi udani weni-weni: ndiwayesa adani.
23. Mundisanthule, Mulungu, nimudziwe mtima wanga; Mundiyeze nimudziwe zolingalira zanga.
24. Ndipo mupenye ngati ndiri nawo mayendedwe oipa, nimunditsogolere pa njira yosatha.

MASALMO 139

Mfundo yaikulu: _____

Mtundu wa kabwerezedwe ka mfundo: _____

KUGAWA NDIME:

MTUNDUWAKABWEREZEDWE

I. _____ Ndime _____

II. _____ Ndime _____

III. _____ Ndime _____

IV. _____ Ndime _____

V. _____ Ndime _____

VI. _____ Ndime _____

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE MOGWIRIZANA NDI PHUNZIRO LA M'MALEMBA

Kukonza mafunso

Ntchito yachisano

- 1. Werengani mawu ochokera pa Marko 6 ndime 45 mpaka 52 kangapo.**
- 2. Werengani mozama malemba a pa ndime-yi**
- 3. Yesetsani kufunsa mafunso omwe angathandize kumvesetsa malemba a pa ndime-yo, kuwathanthauzira komanso kugwiritsa ntchito maphunziro a pa ndimeyo. Wonaninso mafunso-wo ndikusanthula omwe angathandize ophunzira kuphunzira malemba mwandondomeko. Nkoyenera kufunsa mafunso mwandondomeko yomveka bwino.**
- 4. Lembani mafunso-wo mu ndondomeko yomwe muwafunsire. Komalizira kwa funso lili lonse lembani chilembo cha O ngati funso-lo ndilothandiza kumvetsa bwino malemba, I ngati ndilothandiza kutanthauzira malemba komanso A ngati ndilothandiza kugwiritsa ntchito zomwe mwaphunzira.**

Kukonza mafunso okuthandizani kuphunzira malemba

Mukamaphunzira kulemba mafunso okuthandizani kumvetsa malemba mukuphunzira luso. Monga ntchito ina iliyonse, luso lanu lokonza mafunso lizapita patsogolo mukamayeselera. Chofunikira choyamba ndikumvesetsa bwino ndime ya malemba. Kupyolera ku mafunso anu, gulu la ophunzira lanu lizapeza chimene mukufuna. Kuphunzira malo mosazama kuzakupangitsani kufunsa mafunso ndi kukhala ndi zokambirana zosazama. Kuphunzira malemba mozama kuzapangitsa gulu lanu kufunsa mafunso omwe azawathandize kupeza choona cheni cheni cha ndime za malemba ndipo izi zizawayandikitsa kwa Mulungu ndi njira zake. Izi ndiye zotsatira zotamandika za nthawi yomwe tingayiike m'maphunziro a malemba.

- I. Phunzirani moziganizira inu mwini kaye: “Kodi Mulungu akufuna kundiphunzitsa chiyani?” Kenaka ganizirani ena: “Kodi tingapindule chiyani m'miyoyo yathu tikamaphunzirira malemba limodzi.
- II. Mukamaliza kuphunzira, wonaninso chart yanu ndikutsindikiza mfundo zomwe mukudziwa kuti ndizofunikira kuziphatikiza ku maphunziro anu.

Kukonza mafunso okuthandizani kuphunzira malemba

Mukamaphunzira kulemba mafunso okuthandizani kumvetsa malemba mukuphunzira luso. Monga ntchito ina iliyonse, luso lanu lokonza mafunso lizapita patsogolo mukamayeselera. Chofunikira choyamba ndikumvesetsa bwino ndime ya malemba. Kupyolera ku mafunso anu, gulu la ophunzira lanu lizapeza chimene mukufuna. Kuphunzira malemba mosazama kuzakupangitsani kufunsa mafunso ndi kukhala ndi zokambirana zosazama. Kuphunzira malemba mozama kuzapangitsa gulu lanu kufunsa mafunso omwe azawathandize kupeza choona cheni cheni cha ndime za malemba ndipo izi zizawayandikitsa kwa Mulungu ndi njira zake. Izi ndiye zotsatira zotamandika za nthawi yomwe tingayiike m’ maphunziro a malemba.

- I. Phunzirani moziganizira inu mwini kaye: “Kodi Mulungu akufuna kundiphunzitsa chiyani?” Kenaka ganizirani ena: “Kodi tingapindule chiyani m’ miyoyo yathu tikamaphunzirira malemba limodzi.
- II. Mukamaliza kuphunzira, wonaninso ndondomeko yanu ndikutsindikiza mfundo zomwe mukudziwa kuti ndizofunikira kuziphatikiza ku maphunziro anu.
- III. **Kukonza mafunso**

Mafunso anu alozere gulu ku mfundo yaikulu yomwe ikupezeka pa ndime kuti gulu lithe kuvumbulutsa mfundo zomwe ndime ikuphunzitsa ndikulingalira m’ mene angathe kugwiritsira chiphunzitso-cho m’ moyo wawo. Nkoyenera kuzindikira mtundu wa gulu lomwe mukugwira nalo ntchito: Kodi ndi ongobadwanso kumene, kapena ndi okhazikika muuzimu, ndi achichepere kapena ndi akulu. Gulu likuyenera kudutsanso momwe inu mwadutsa kale pokonzekera maphunziro; mafunso anu athe kuthandiza gulu kumvesetsa zomwe inu mwafukula pa nthawi yomwe mumakonzekera maphunziro.

- A. Yambani ndi mafunso othandiza gulu kudziwa zambiri pa ndime. (Kodi akukhudzidwa ndi ndani? Ali kuti? Akuchita chiyani?)
- B. Kupyolera m’ mafunso anu litsogolereni gulu mwa ndondomeko kuwunikiranso ndime kuchokera koyamba mpaka komalizira. Mutha kutsogolera gulu kuwunika gawo ndi gawo la ndime ndikuwawunikira kugwirizana pakati pa magawo.
- C. **Funsani: Mafunso othandiza kumvesetsa malemba (Mfundo)**
Mafunso othandiza kutanthauzira malemba
Mafunso othandiza kuchita zomwe malemba aphunzitsa.

Mafunso othandiza kumvesetsa malemba

- Thandizani gulu kuwona zomwe ndime ikunena
- Kupyolera mnjira zosiyanasiyana tsogolerani gulu kuti liwone anthu omwe akukhudzidwa ndi nkhani yomwe ili m'ndime, zomwe zikuchitika, nthawi yomwe zikuchitikira komanso malo omwe zikuchitikira.
- Gulu lithe kufotokoza anthu omwe ali m'ndime kapena zochitika zomwe ndime ikunena.
- Lithandizeni gulu kulingalira kuti ali m'zochitika zomwe ndime ikufotokoza. Mwachitsanzo, anthu aziwone ngati iwowo ndi Aefeso akulandira kalata yochokera kwa Mtumiki Paulo.
- Litsogolerani gulu kuwona zinthu zina zokhudza ndime zomwe inu mwaziwona: Monga kusiyana kwa makhalidwe a anthu awiri ndi zina zotero.

Mafunso othandiza kutanthauzira malemba

- Tsogolerani gulu kuwunika malemba mwakuya ndikufunsa mafunso omwe angawathandize kupeza choona cheni cheni monga 'Chifukwa chiyani izi zinachitika?'
- Gulu likuyenera kugwirizana tanthauzo la mawu ndi ziganizo zina
- Thandizani gulu kuwona zolinga za mitundu ya kalembedwe. (Funsani mafunso malingana ndi momwe inu munatanthauzira malemba kuchokera m'ndondomeko yanu yomvesetsa malemba. Iyinso ndi njira yothandiza gulu lanu kulumikiza zomwe magawo a ndime akunena).
- Gulu likapeza choonadi pa ndime, mafunso anu alithandize kuganizira mozama malemba a pa ndime-yo.

Mafunso othandiza kuchita zomwe malemba aphunzitsa

- Mafunso awa amathandiza mamembala a gulu kuganizira zomwe angasinthe m'miyoyo yawo kuti akhale moyo ogwirizana ndi zomwe malemba akuphunzitsa. Zina mwa zinthu-zi ndi makhalidwe, ma ubwenzi komanso ntchito zawo.
- Funsani mafunsowa kuchokera ku matanthauzo a mfundo zikuluzikulu ndipo mafunsowa abwere pamene gulu lapeza choonadi. Zindikirani kuti nzothandiza kukhala ndi mafunso a mtundu-wu ochepa apo ndi apo pomwe tikuphunzira malemba osati ambiri-mbiri pena paliponse.

MARKO 6 NDIME 45 MPAKA 52

45) Ndipo pomwepo Iye anakangamiza ophunzira ache alowe m'ngalawa, ndi kumtsogolera kutsidya lija la Betsaida, m'mene Iye yekha ali mkuuza khamulo kuti amuke.

46) Ndipo atalawirana nawo, anachoka Iye, nalowa m'phiri kukapemphera.

47) Ndipo pofika madzulo ngalawa inali pakati pa nyanja, ndi Iye yekha pamtunda.

48) Ndipo pakuwona ali kuvutidwa ndi kupalasa, pakuti mphepo inadza nikhomana nawo, pa ulonda wachinayi wa usiku Iye anadza kwa iwo, alikuyenda pamwamba pa nyanja; nati awapitilire;

49) Koma iwo, pamene anamuwona alikuyenda panyanja, anayesa kuti ndi muzukwa, nafuula:

50) Pakuti iwo onse anamuwona Iye, nanthunthumira. Koma pomwepo anawalankhula nanena nawo, Limbani mtima; ndinetu musaope.

51) Ndipo Iye anakwera, nalowa kwa iwo m'ngalawa, ndipo mphepo inaleka; ndipo anadabwa kwakukuru mwa iwo okha;

52) Pakuti sanazindikira za mikateyo, koma mitima yawo inauma.

DONGOSOLO YAKAPANGIDWE KA MAFUNSO

Kuchokera ku ndondomeko yomwe mwakonza kale, pangani mafunso kuchokera pa mutu wina uliwonse. Zomwe mwalemba pansu pa mutu uliwonse zigwirizane ndi mafunso omwe mulembe.

(O) Mvesetsani malemba	(I)Tanthauzirani malemba	(A) Zomwe mungachite malinga ndi phunziro la m'malemba
<div style="border: 1px solid black; padding: 5px; margin-bottom: 10px;"> Mfundo yoyamba Ndime 1 - Mvesetsani - Mvesetsani - Mvesetsani Ndime 2 - Mvesetsani - Mvesetsani </div> Mfundo yachiwiri Ndime 3-Mvesetsani	Tanthauzirani m'mene mukumvela malemba apa	Lembani zomwe mungachite pokwaniritsa tanthauzo la malemba apa -Ndipange chiyani? -Ndipange bwanji? (Perekani zitsanzo zomveka bwino)

(Pa tsamba lina)

Lembani ndandanda wa mafunso (Kuchokera pa ndondomeko yomwe mwapanga kale).

Ndime...Mfundo yoyamba yomvesetsa malemba

- 1. Funso lomvesetsa (Akukhudzidwa ndi ndani? Amapanga chiyani?)
- 2. Funso lomvesetsa (Anali kuti?)
- 3. Funso lomvesetsa (Chinachitika ndi chiyani)

(Pambuyo pa mafunso omvesetsa malemba angapo funsani funso limodzi kapena awiri otanthauzira ndime)

- I 4. Funso lotanthauzira malemba (Kodi Yesu ananeneranji..?)
- I 5. Funso lotanthauzira malemba (Paulo amatanthauza chiyani pomwe anati...?)

(Mukafunsa mafunso omvesetsa malemba komanso otanthauzira ndime angapo nkwabwino kufunsa mafunso angapo othandiza kukwaniritsa malemba. Mafunsowa agwirizane ndi choona chenicheni chomwe mafunso omvesetsa ndi kutanthauzira malemba avumbulutsa.)

- A 6. Funso lokwaniritsa malemba (Yankho la funsoli zikhale ntchito zomwe munthu angachite pokwaniritsa malemba. Kodi ndingachitenji kuti ndifanane ndi Yesu?)

KONZANI:

Mafunso othandiza kumvesetsa malemba kuchokera pa mutu wa ‘O’ m’ndondomeko yanu.

Mafunso othandiza kutanthauzira malemba kuchokera pa mutu wa ‘I’ m’ndondomeko yanu.

Mafunso othandiza kuchita zomwe malemba aphunzitsa kuchokera pa mutu wa ‘A’ m’ndondomeko yanu.

Zomwe zingakuthandizeni kukonza mafunso abwino:

Lembani mafunso anu mwatsatanetsatane kuchokera loyamba mpaka lomaliza. Lembani mafunso-wa motsatira m’mene alili m’ndondomeko yanu.

Mafunso akhale osavuta komanso atchutchutchu, olozera anthu ku mayankho omwe angawapeze m’malemba.

Mafunso apangitse anthu kukambilana komwe kuwapangitse kumvetsa tanthauzo la malemba.

Mafunso akhale mu ndandanda wake mwadongosolo, momveka bwino

Mafunso akhale ndi mayankho kuchokera mu malemba.

Funso lililonse likhaleli pansu pa mitu itatu imeneyi, ‘O’ (Othandiza kumvetsa), ‘I’ (Othandiza kutanthauza), komanso ‘A’ (Othandiza kuchita zomwe taphunzira).

(Wonaninso phunziro 5)

MARKO 6 NDIME 45 MPAKA 52

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

Ndandanda wa mafunso

Lembani ndandanda wa mafunso

omwe mukuganiza kuti akuthandizani kumvetsa, kutanthauzira
ndikukwaniritsa malemba. Musazipanikize kulemba m' malo onse.

1. _____
2. _____
3. _____
4. _____
5. _____
6. _____
7. _____
8. _____
9. _____
10. _____
11. _____
12. _____
13. _____
14. _____
15. _____

Ndandanda wa mafunso

Lembani ndandanda wa mafunso

omwe mukuganiza kuti akuthandizani kumvetsa, kutanthauzira
ndikukwaniritsa malemba. Musazipanikize kulemba m' malo onse.

16. _____

17. _____

18. _____

19. _____

20. _____

21. _____

22. _____

23. _____

24. _____

25. _____

26. _____

27. _____

28. _____

29. _____

30. _____

Mafanizo

Ntchito yachisanu ndi chimodzi

- 4. Werengani mawu ochokera pa Marko 4 ndime 1 mpaka 20 kangapo.**
- 5. Dulirani mawu-wo pogwiritsa ntchito njira yosavuta yodulira malemba**
- 6. Pezani mfundo yomwe akutsindika m'fanizo-lo.**
- 7. Werengani mozama fanizo lomwe mwadulira-lo. Tanthauzirani fanizo-lo monga alitanthauzira m'ndimeyo.**
- 8. Pangani mafunso anu othandiza kumvesetsa, kutanthauzira komanso kukwaniritsa fanizo-lo.**

Fanizo ndi nthano yaifupi yomwe imakamba za zinthu zochitika tsiku ndi tsiku m'moyo ndi cholinga cholongosola choona cheni-cheni cha moyo wa uzimu. Yesu nthawi zambiri amaphunzitsa kupyolera mafanizo choncho nkoyenera kuti tizimvetsa bwino bwino zomwe mafanizo akufuna kutiwuza. Pomwe Yesu amaphunzitsa kupyolera m'mafanizo panalinsu cholinga china chowonjezera. Amafuna kubisa choona cheni-cheni kwa anthu omwe samalabadira ndikuwonetsa choona cheni-cheni kwa iwo olabadira.

Zindikirani kuti pomwe zochitika m'mbiri yakale tingazigwiritse ntchito kufotozozera malemba, mafanizo ndi nthano yapadera yopangidwa ndi cholinga chophunzitsa choonadi. Ngakhale fanizo si chinthu choti chinachitika m'mbiri yakale koma pongotchula kuti fanizo zikutanthauza kuti ndi zinthu zoti zimachitika m'moyo.

ZOLOZERA ZINAYI ZOTHANDIZA KUTI TIMVETSE MAFANIZO

1. Yambirani pa zomwe mukudziwa za nkhaniyo:

- a) Kodi nkhaniyi anayikamba pa mwambo wanji? (Luka 15 ndime 1 mpaka 2)
- b) Kodi tanthauzo la fanizo-lo akulifotokoza bwanji? (Luka 15 ndime 7 ndi 10, Mateyu 24 ndime 44 komanso Mateyu 25 ndime 13).

2. Pezani mfundo yomwe akuyitsindika m'fanizolo:

Wonani zomwe malemba akunena asanakambe fanizolo komanso pambuyo pa fanizolo

- a) Luka 15 ndime 4-Nkhosa yosokera
- b) Luka 15 ndime 8 mpaka 10-Ndalama yotayika

3. Pezani mawu opanda ntchito

Zindikirani zomwe mawu akukamba koma cholinga chake sikuphunzitsa choonadi (Luka 17 ndime 7 mpaka 9).

- a) Luka 15 ndime 4- Nkhosa makumi-makumi zosatayika
- b) Luka 15 ndime 8- Ndalama zisanu ndi zinayi zosatayika

4. Zindikirani mawu ofunikira

Zindikirani kuti mawu omwe cholinga chake ndi kuphunzitsa choonadi amawabwereza potsindikiza phunziro lalikulu la fanizo.

MARKO 4 NDIME 1 MPAKA 20

1. Ndipo anayambanso kuphunzitsa pambali pa nyanja. Ndipo anasonkhana kwa Iye khamu lalikulurikuru, kotero kuti analowa Iye mu ngalawa, nakhala m'nyanja; ndipo khamu lonse linakhala pamtunda m'mbali mwa nyanja.
2. Ndipo anawaphunzitsa zinthu zambiri m'mafanizo, nanena nawo m'chiphunzitso chake,
3. Mverani: taonani wofesa anaturuka kukafesa;
4. Ndipo kunali m'kufesa kwake, zina zinagwa m'mbali mwa njira, ndi mbalame zinadza ndi kuzitha kudya.
5. Ndipo zina zinagwa pa nthaka yathanthwe, pamene panalibe nthaka yambiri; ndipo pomwepo nzinamera, chifukwa zinalibe nthaka yakuya;
6. Ndipo litakwera dzuwa zinapsereera; ndipo popeza zinalibe mizu, zinakhwinyata.
7. Ndipo zina zinagwa pa minga, ndipo minga inakula, nizitsamwitsa, ndipo sizinabala zipatso.
8. Ndipo zina zinagwa m'nthaka yabwino, ndipo zinapatsa zipatso, ndi kukula ndikuchuluka; ndipo zinabala ndikupindula makumi atatu, ndi makumi asanu ndi limodzi, ndi khumi.
9. Ndipo ananena, amene ali nawo makutu akumva amve.
10. Ndipo pamene anakhala payekha, iwo amene anali pafupi ndi Iye pamodzi ndi khumi ndi awiriwo anamfusa za mafanizo.
11. Ndipo Iye ananena nawo, Kwa inu kwapatsidwa chinsinsi cha Ufumu wa Mulungu; koma kwa iwo ali kunja zonse zichitidwa m'mafanizo;
12. Kutu kupenya, apenye koma asazindikire; ndipo amve, koma asadziwitse; kutu pena angatembenuke, ndikukhululukidwa.
13. Ndipo ananena nawo, simudziwa kodi fanizo ili? Mukazindikira bwanji mafanizo onse.
14. Wofesa afesa mawu.
15. Ndipo iwo ndiwo a m'mbali mwa njira mofesedwamo mawu; ndipo pamene anamva, pomwepo akudza Satana nachotsa mawuofesedwa mwa iwo.
16. Ndipo momwemonso iwo ndiwo amene afesedwa pathanthwe, atamva mawu awalandira pomwepo ndikusekera;
17. Ndipo alibe mizu mwa iwo okha, koma akhala kanthawi; pamenepo pakudza masautso kapena mazunzo chifukwa cha mawu, pomwepo akhumudwa.
18. Ndipo ena ndiwo afesedwa kuminga; iwo ndiwo amene adamva mawu,
19. Ndipo malabadiro a dziko lapansi, ndi chinyengo cha chuma, ndikulakalaka kwa zinthu zina, zilowamo, zitsamwitsa mawu, ndipo akhala opanda chipatso.
20. Ndipo iwo ofesedwa pa nthaka yabwino ndiwo oterewa akumva mawu, nawalandira, nabala zipatso zakupindula makumi atatu, ndi makumi asanu ndi limodzi ndi makumi khumi.

FANIZO LA OFETSA

MARKO 4 ndime 1 mpaka 20

I. KUDULIRA FANIZO

A. _____ NDIME _____

B. _____ NDIME _____

C. _____ NDIME _____

D. _____ NDIME _____

II. KODI FANIZO LIKUTSINDIKIZA MFUNDO YANJI?

III. NDONDOMEKO YOMVETSA FANIZO MOZAMA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

Ndandanda wa mafunso a Fanizo Lembani ndandanda wa mafunso
omwe mukuganiza kuti akuthandizani kumvetsa, kutanthauzira
ndikukwaniritsa malemba. Musazipanikize kulemba m' malo onse.

1. _____

2. _____

3. _____

4. _____

5. _____

6. _____

7. _____

8. _____

9. _____

10. _____

11. _____

12. _____

13. _____

14. _____

15. _____

16. _____

Ndandanda wa mafunso a fanizo Lembani ndandanda wa mafunso
omwe mukuganiza kuti akuthandizani kumvetsa, kutanthauzira
ndikukwaniritsa malemba. Musazipanikize kulemba m' malo onse.

17. _____

18. _____

19. _____

20. _____

21. _____

22. _____

23. _____

24. _____

25. _____

26. _____

27. _____

28. _____

29. _____

30. _____

31. _____

Kulosela

Ntchito yachisanu ndi chiwiri

Zoloserera zimapezeka m'malemba kuchokera bukhu la Genesis mpaka Chivumbulutso

- ✓ Pafupifupi ndime imodzi mwa ndime zitatu zili zonse ku chipangano chakale ndi zoloserera za mtsogolo
- ✓ Pafupifupi ndime imodzi mwa ndime zisanu zili zonse ku chipangano chatsopano ndi zoloserera za mtsogolo
- ✓ Choncho pafupifupi ndime imodzi pa ndime zinayi zili zonse m'Baibulo ndi zoloserera za mtsogolo.

Kuchuluka kwa ndime zoloserera m'Baibulo kukusonyeza kuti Mulungu amatsindikiza kufunika kwa ulosi.

I. Chinthu choyamba kwa ophunzira aliyense wa malemba ndikuzindikira mtundu wa ulosi omwe uli m'malemba omwe akufuna kuphunzira.

Pali mitundu iwiri ya ulosi

A. Olosera za mtsogolo

B. Olosera za chikhalidwe-kulosea za makhalidwe, machitidwe oyenera ndi choonadi cha malemba

Zolosea zina zimaphatikiza mitundu yonse iwiri. Pa Zekariya 1 ndime 1 mpaka 15 akulosea za makhalidwe, machitidwe oyenera ndi choonadi cha malemba koma masomphenya otsatirawo pa ndime 16 mpaka 21 akulosea za mtsogolo. Malemba ambiri opezeka pa Zekariya 7 akulosea za chikhalidwe koma magawo otsatirawo akulosea za mtsogolo. Ulosi wambiri umalosea za mtsogolo.

II. Nazi zokuthandizani pomwe mukufuna kumvesetsa ndime zolosea za mtsogolo.

A. CHINENERO CHA TSIKU NDI TSIKU: Werengani ndimeyo mosaganizira mozama, kutanthauzira mawuwo m'mene mukuwamvera, mwatchutchutchu ngati palibe choletsa kuteru. Maulosi a zochitika mtsogolo atanthauzireni monga m'mene awalembera osawawona ngati chining'a ayi. Athanthauzireni mosavuta, mwatchutchutchu-Zomwe akunena ndi zomwe akutanthauza.

B. CHINING'A: Phunzirani kusiyantsa mawu amasiku onse ndi chining'a koma tsatirani zomwe mukudziwa za chinenero posiyantsa mawu wamba ndi chining'a.

1. Mawu ena nkoyenera kuwamvetsa kuti ndi chining'a chifukwa kusatero kutha kukusokonezani. Mwachitsanzo, Yoweli 2 ndime 31-mwezi uzasanduka mwazi; Yesaya 11 ndime 1-mphukira pa tsinde la Jese; Zekariya 4 ndime 7-phiri kuchotsedwa.

2. Tmatchula kufotokozera uku ‘chithunzi cha mawu’ monga m’mene tiwonera pa Daniel: mkango wa mapiko, kambuku wa mapiko anayi.
3. Cholinga ndi kulingalira kuti chining’a chikutanthauza chiyani chifukwa chinthu chomwe chikutchulidwa m’chining’a chikukwaniritsa chinthu cheni-cheni mu mbiri.

Zitsanzo:

Daniel 7 ndime 17-Zirombo zinayi zikuyimilira mafumu anayi omwe adzauka pa dziko lapansi; Yohane 2 ndime 19-Yesu akulosea kuuka kwake m’manda pa tsiku lachitatu pomwe akuti, “Pasulani kachisi uyu, ndipo masiku atatu ndidzamuutsa.

C. CHENJEZO

Kuzindikira mtundu wa ulosi m’malemba ena kumakhala kovuta

Chitsanzo: Amosi 9 ndime 13 mpaka 15. Zikuwoneka kuti ndime iyi nkofunika kuyimvetsa ngati chining’a. Koma monga m’mene tanenera, nkoyenera kumvetsa ulosi mwatchutchutthu osati ngati chining’a. Komabe malemba ambiri olosera ali m’chining’a choncho nkofunika kuphunzira kusiyantsa chining’a ndi mawu wamba.

D. Maulosi amaphatikiza zochitika m’mbuyo, zomwe zikuchitika pano komanso zomwe zizachitike mtsogolo. Maulosi satsatira ndondomeko ya m’mene zinthu zimayendera, amatha kukamba za mtsogolo kenaka za pa mbuyo.

Ntchito yachisanu ndi chiwiri.

- 1. Werengani mawu ochokera pa Yesaya 1 ndime 1 mpaka 31 kangapo.**
- 2. Dulirani mawu-wo pogwiritsa ntchito njira yosavuta yodulira malemba.**
- 3. Siyanitsani mitundu ya maulosi yomwe ikupezeka m'ndimeyo.**
- 4. Pezani mfundo yaikulu ya ulosi-wu.**
- 5. Werengani mozama ndime yomwe mwadulira-lo.**
- 6. Pangani mfundo zikuluzikulu za ulaliki omwe mungatenge pa malemba amenewa. Tengani mfundo yoyamba ndipo iwunikireni ndime kwa ndime. Pa mfundoyi, fotokozani ndime zonse za malemba-wa zomwe zikufotokozera mfundoyi. Nkoyenera kufotokoza mawu ndi ziganizo zomwe mwazimvesetsa, mwazitanthauzira komanso zomwe mwazikwaniritsa. Pangani chimodzimodzi ku mfundo zotsatira. Ganizirani nthano zomwe zingakuthandizeni kufotokozera mfundo-zi.**

YESAYA 1 ndime 1 mpaka 31

1. Masomphenya a Yesaya mwana wa Amози, amene iye anawona, onena za Yuda ndi Yerusalemu, masiku a Uziya, Yotamu, Ahazi, ndi Hezekiya mafumu a Yuda.
2. Imvani miyamba inu, tchera makutu, iwe dziko lapansi, chifukwa Yehova wanena, Ndakulitsa ndipo ndalera ana, ndipo iwo anandipandukira ine.
3. Ng'ombe idziwa mwini wake ndipo buru adziwa pomtsekereza; koma Israyeli sadziwa, anthu anga sazindikira.
4. Mtundu wochimwa inu, anthu olemedwa ndi mphulupulu, mbewu akuchita zoipa, ana amene achita moononga, iwo amsiya Yehova, iwo amnyoza Woyera wa Israyeli, iwo adana naye nabwerera m'mbuyo.
5. Nanga bwanji mukali chimenyedwere kuti inu muli kundipandukirabe? Mutu onse ulikudwala, ndi mtima wonse walefuka.
6. Kuchokera pansu pa phazi kufikira kumutu m'menemo mulibe changwirowo; koma mabala, ndi mikwingwirima, ndi zironde; sizinapole, ngakhale kumangidwa, ngakhale kupakidwa mafuta.
7. Dziko lanu liri bwinja; midzi yanu yatenthedwa ndi moto; dziko lanu alendo alimkudya pamaso panu; ndipo liri labwinja mongalagubuduzidwa ndi alendo.
8. Ndipo mwana wamkazi wa Ziyoni wasiyidwa ngati chitando cha m'munda wamphesa, ngati chilindo cha m'munda wamankhaka, ngati mudzi wozingidwa ndi nkondo.
9. Akadapanda Yehova wamakamu kutisiyira otsala ang'ono-ang'ono ndithu, ife tikanakhala ngati Sodomu, ife tikadanga Gomora.
10. Imvani mawu a Yehova inu olamulira a Sodomu, tcherani makutu ku chilango cha Mulungu wathu, inu anthu a Gomora.
11. Nditani nazo nsembe zanu zochulukazo? Ati Yehova; ndakhuta nazo nsembe zopsereza za nkhoa za mphongo ndi mafuta a nyama zonenepa; sindisekera ndi mwazi wa mwazi wa ng'ombe za mphongo, ngakhale wa ana ankhoa, ngakhale wa atoned.
12. Pakudzaonekera inu pamaso pa Ine, ndani wafuna chimenechi m'dzanja lanu, kupondaponda m'mabwalo mwanga?
13. Musadze nazonso, nsembe zachabechabe, nsembe zofukiza zondinyansa; tsiku lokhala mwezi ndi sabata, kumema masonkhano.
14. Masiku ano okhala mwezi ndi nthawi za mapwando anu mtima wanga uzida; zindivuta Ine; ndalema ndi kupilira nazo.
15. Ndipo pamene mutambasula manja anu, ndidzakubisilani inu maso anga; ine pochulukitsa mapemphero anu Ine sindidzamva; manja anu adzala mwazi.
16. Sambani, dziyereseni; chotsani machitidwe anu oipa pamaso panga; lekani kuchita zoipa;
17. Phunzirani kuchita zabwino; funani chiweruzo; thandizani osautsidwa, weruzirani ana amasiye, munenere akazi amasiye.
18. Tiyeni tsono tiweruzane, ati Yehova; ngakhale zoipa zanu zili zofiira, zidzayera ngati matalala; ngakhale ziri zofiira ngati kapezi, zidzakhala ngati ubweya wa nkhoa, woti mbu.
19. Ngati inu muli ofuna ndi omvera, mudzadya zabwino za dziko,

20. Koma ngati mukana ndi kupanduka, mudzathedwa ndi lupanga; chifukwa mkamwa mwa Yehova mwatero.
21. Mudzi okhulupirika wasanduka wadama! Wodzala chiweruzowo! Chilungamo chinakhala koma tsopano ambanda.
22. Siliva wako wasanduka mphala, vinyo wako wasanganizidwa ndi madzi.
23. Akuru ako apanduka, ali anzawo a mbala; onse akonda mitulo, natsala zokometsera milandu; iwo saweruzira amasiye; ngakhale mlandu wa mkazi wamasiye suwafika.
24. Chifukwa chake Yehova ati, Yehova wamakamu wa mphamvu wa Israyeli, Ha! Ndidzatonthoza mtima wanga pochotsa ondivuta, ndikubwezera chilango adani anga;
25. Ndipo ndidzaikanso dzanja langa pa iwe, ndi kukusungunula kukusiyanitsa iwe ndi mphala yako, ndipo ndidzachotsa seta wako wonse;
26. Ndidzabweza oweruza ako monga poyamba, ndi aphungu ako monga pachiyambi; pambuyo pake udzatchedwa, Mudzi okhulupirika.
27. Ziyoni adzawomboledwa ndi chiweruzo, ndi otembenuka mtima ake ndi chilungamo.
28. Koma kupasula kwa olakwa ndi kwa ochimwa kudzakhala kumodzi, ndi iwo amene asiya Yehova adzathedwa.
29. Chifukwa adzakhala ndi manyazi, chifukwa cha mtengo yathundu munaikhumba, ndipo inu mudzagwa nkhope, chifukwa cha munda imene mwaisankha.
30. Chifukwa mudzakhala ngati mtengo wathundu, umene tsamba lake linyala, ngatinso munda wopanda madzi.
31. Ndipo wamphamvu adzakhala ngati chingwe chabwazi ndi ntchito yake ngati nthethe; ndipo zones zidzayaka moto pamodzi, opanda wozimitsa.

CHITSANZO

Kudulira malemba a ulaliki

(Kugwiritsa ntchito Masalmo 1 ngati chitsanzo)

MAWU OYAMBA: Cholinga cha mawu awa ndikufuna kuwapatsa anthu chidwi chomvetsera komanso kuwawonetsa komwe uthenga ukuloza.

- 1) Perekani mbiri ya malemba omwe mukufuna kugawana nawo, kuwadziwitsa nthawi yomwe izi zinachitika ndi zina zambiri zokhudza ndime-yo.
- 2) Nenani mfundo yaikulu ya ndimeyo ndipo fotokozani momveka bwino pogwiritsa ntchito zitsanzo za makono kuti anthu amvesetse.

CHITSANZO:

“Ili ndi Salmo lotiwuza zochita lomwe linalembedwa ndi mlembi yemwe sakudziwika lokhudza njira ziwiri za moyo.... mwachidziwikire tapatsidwa mwayi opanga chisankho.... chotenga njira yabwino yomwe izatitengere ku chisangalalo..

- ✓ **TUNTHU LA MAWU**-Uwu ndi mtima wa uthenga wanu motsatira m'mene mwadulira ndime. Gwiritsani ntchito mitu ya ndondomeko yanu ngati mfundo zikuluzikulu za uthenga wanu. Pa mutu uliwonse (Kumvesetsa malemba, kutanthauzira malemba komanso kukwaniritsa malemba) tengani ndime zingapo za m'Baibulo zomwe zikuthandizeni kulungosola mfundo yaikulu ya mutu umenewo. Gwiritsani ntchito zitsanzo polungosola mfundo zanu mogwirizana ndi mfundo yaikulu ya mutu. Wonani chitsanzo chili pansipa.

I. Munthu Odala-Ndime 1 mpaka 3: Mu ndime zimenezi tikuwona tanthauzo la munthu odala (Kodi ndi otani, amapanga chiyani ndipo amakwaniritsa chiyani). Pa ndime 1 ndi 'munthu odala' yemwe amakhala m'chikondwerero choonadi, “sayenda....kapena kuyimilira....kapena kukhala....” Mnjira za ochimwa (Chitsanzo cha kubwerezabwereza mawu kwa kalembedwe ka chi-Heberi) koma “m'chilamuliro cha Yehova muli chikondwerero chake.” “Ndiye akunga mtengo wooka pa mtsinje wa madzi,” Kutipatsa chithunzithunzi cha chisamaliro ndi ulemelero umene Mulungu amapatsa anthu ake.

II. Munthu oyipa-Ndime 4 mpaka 6: “Oyipa satero ayi..” Ndime 4 ikufotokoza machitidwe a anthu osalungama. Alibe chikondwerero mu malamulo a Mulungu. Pomwe odala ali ngati mitengo ya zipatso za mtengo wapatali, anthu oyipa ali ngati mungu wouluka ndi mphepo, alibe gawo pa Mulungu. Pa ndime 5 mpaka 6

tiwerenga tsoka lomwe likuwayembekeza oyipa komanso tsogolo labwino lomwe odala awakonzera.

MAWU OMALIZA: Apa tikufuna titsendere uthenga wathu pomanga nkota wa zonse zomwe takamba pa mfundo yathu yaikulu ndikuphunzitsa ndi cholinga choti anthu akwaniritse malemba popereka zitsanzo za m'mene anthu angachite zomwe aphunzira.

Chitanso:

“Tiyeni tikhale ndi chilakolako cha mawu a Chauta, madalitso amene munthu odala amalandira atilimbikitse ife kufunafuna Mulungu ndi kugawana mawu ake ndi otsokera.”

ZINDIKIRANI ICHI: Ndime zonse zomwe tawerenga pa uphunzitsi wathu komanso zitsanzo zomwe tagwiritsa ntchito pofotokoza zigwirizane ndi mfundo yaikulu ya chiphunzitso chathu.

Yesaya 1

Mfundo yaikulu _____

KUDULIRA

MTUNDU WA ULOSI

I. _____ NDIME _____

II. _____ NDIME _____.

III. _____ NDIME _____

IV. _____ NDIME _____

V. _____ NDIME _____

VI. _____ NDIME _____

VII. _____ NDIME _____

VIII. _____ NDIME _____

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

Ndondomeko ya ulaliki

Pogwiritsa ntchito ndondomeko yomwe mwapanga kale pano mutha tsopano kukonza ndondomeko ya ulaliki wanu.

Mutu wa
ulaliki: _____

Bukhu: _____ Ndime _____

I. Mawu oyamba a ulaliki

Yambani ndi nthano, ndakatulo kapena mawu a nthabwala musanayambe kulalikira. Izi zikhale zogwirizana ndi malemba omwe mukufuna kulalikira.

II. Tunthu la uthenga

Potsatira ndondomeko yanu, werengani ndime zonse zomwe mwazisanthula kale.

Tsatirani ndondomeko yanu polongosola uthenga wanu.

ZINDIKIRANI: Si malemba onse omwe ali pansu pa mutu ‘omvesetsa mawu’ akuyenera kutanthauziridwa kapena kukwaniritsidwa.

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

(Pangani chimodzimidzi pa ndime zonse)

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

III. Mawu omaliza

Pogwiritsa ntchito mfundo zomwe mwazisanthula kale, mangani nkota mfundo zikuluzikulu za ulaliki wanu ndipo atsogolereni anthu m'mene angakwaniritse zomwe aphunzira.

Ndime zolongosola

- 1. Werengani malemba omwe ali pa Yohane 13 ndime 1 mpaka 20 kangapo**
- 2. Yankhani mafunso omwe ali pa tsamba 48.**

Yohane 13 ndime 1 mpaka 20

- 1) Koma pasanafike phwando la Paskha, Yesu podziwa kuti nthawi yake idzadza yakuchoka kuturuka m'dziko lino lapansi, kunka kwa Atate, m'mene anaconda ake a Iye yekha a m'dziko lapansi, anawakonda kufikra chimariziro.
- 2) Ndipo pokhala pa mgonero, mdierekezi adatha kuyika mu mtima wake wa Yudase mwana wa Simoni Isikariote, kuti akampereke Iye ,
- 3) Yesu podziwa kuti Atate adampatsa Iye zonse m'manja mwake, ndi kuti anachokera kwa Mulungu, namuka kwa Mulungu,
- 4) Ananyamuka pa mgonero, navula Malaya ake; ndipo m'mene adatenga chopukutira, anadzimanga mchiuno.
- 5) Pomwepo anathira madzi m'nsambidwe, nayamba kusambitsa mapazi akuphuzira ake, ndikuwapukuta ndi chopukutira, chimene adadzimanga nacho.
- 6) Anadza pomwepo kwa Simoni Petro. Iyeyo anena ndi Iye, Ambuye, kodi inu mundisambitsa ine mapazi?
- 7) Yesu anayankha nati kwa iye, chimene ndichita Ine suchidziwa tsopano; koma udzadziwa m'tsogolo mwake.
- 8) Petro ananena ndi Iye, simudzasambitsa mapazi anga ku nthawi yonse. Yesu anamyankha iye, ngati sindikusambitsa iwe ulibe cholandira pamodzi ndi Ine.
- 9) Simoni Petro ananena ndi Iye, Ambuye, simapazi anga okha, komanso manja ndi mutu.
- 10) Yesu ananena naye, amene anatha kusamba alibe kusowa koma kusamba mapazi, koma ayera monse: ndipo inu ndinu oyera, koma si nonse ayi.
- 11) Pakuti anadziwa amene adzampereka Iye; chifukwa cha ichi anati simuli oyera nonse.
- 12) Pamenepo, atatha Iye kusambitsa mapazi awo, ndikutenga Malaya ake, anaseyamanso, nati kwa iwo, nanga chimene ndakuchitirani inu, muchizindikira kodi?
- 13) Inu munditcha ine Mphunzitsi, ndi Ambuye: ndipo munena bwino; pakuti ndine amene.
- 14) Chifukwa chake, ngati Ine Ambuye ndi Mphunzitsi, ndasambitsa mapazi anu, inunso muyenera kusambitsa mapazi wina ndi mzake.
- 15) Pakuti ndakupatsani inu chitsanzo, kuti monga Ine ndakuchitirani inu, inunso muchite.

- 16) Indetu, indetu ndinena ndi inu, kapolo sali wamkulu ndi mbuye wake; kapena mtumwi sali wamkuru ndi womtuma iye.
- 17) Ngati mudziwa izi, odala inu ngati muzichita.
- 18) Sindinena za inu nonse; ndidziwa amene ndawasankha: koma kuti cholemba chikwaniridwe, Iye wakudya mkate wanga anatsalimira pa Ine chidendene chake.
- 19) Kuyambira tsopano ndinena kwa inu, chisadachitike, kuti pamene chitachitika, musakhulupilirwe kuti ndine amene.
- 20) Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Iye wolandira amene ali yense ndimtuma, andilandira Ine; koma wolandira Ine alandira wondituma Ine.

Ntchito yowonjezera yoyamba

‘O’ akuyimilira funso lothandizira kumvetsa

‘I’ akuyimilira funso lothandizira kutanthauzira

‘A’ akuyimilira funso lothandiza kukwaniritsa

MAFUNSO OTHANDIZA KUMVESETSA NDIME

O (1). Kodi anthu omwe akukhudzidwa m’nthano-yi ndi ndani? _____

O (2). Kodi chimafuna kuchitika ndi chiyani?

I (3). Kodi phwando la Paskha ndi chiyani?

O (4). Longosolani m’mene mukumvera nkhanayi.

O (5). Kodi Yesu amadziwa za Iye zotani zomwe azitchula m’ndime yoyamba _____

I (6). Kodi yesu ankawakonda bwanji ophunzira ake?

I (7). Kodi Yesu amakondanso Yudase Isikariote chimodzimodzi? _____

I (8) Kodi mkotheke Yesu kukonda munthu amene amakonza zomupereka?

O (9) Tchulani zomwe Yesu amadziwa za Iye mwini zomwe azilemba pa ndime 3

I (10) Kodi n'chifukwa chiyani Yesu anasambitsa mapazi a ophunzira?

I (11) Kodi ndi ntchito ya ndani kusambitsa mapazi?

O (12) Kodi Petro anawuza Yesu zotani pomwe amamusambitsa mapazi?

I (13) Ndi chifukwa chiyani Petro sakufuna Yesu kuti amusambitse mapazi?

O (14) Kodi Petro anayankha kuti chiyani pa zomwe Yesu anamyankha mu ndime 9?

I (15) Fotokozani zomwe Yesu akutanthauza pa mawu omwe akupezeka pa ndime 10

A (16) Mungayankhe bwanji funso lomwe Yesu akufunsa pa ndime 12?

I (17) Kodi Yesu akuneneranji kuti tidzisambitsana mapazi wina ndi mzake?

I (18) Kodi Yesu amathanuza chiyani ndi mawu omwe anayankhula m'ndime 16?

I (19) Kodi nkosakwanira bwanji kumangodziwa zinthu (Werengani ndime 17)?

I (20) Kodi Yesu akukamba za ndani m'ndime 18?

I (21) Kodi Tanthauzirani malemba omwe ali pa ndime 20.

I (22a) Mungakwaniritse bwanji phunziro lalikulu la malemba-wa?

A (22b) Malemba-wa angakwaniritsidwe bwanji?

A (22c) Kodi ndi zinthu zotani zomwe mungapange pokwaniritsa malemba-wa?

Ntchito yowonjezera yachiwiri

Werengani mawu ochokera pa Filemoni kangapo.

Dulirani mawu-wo pogwiritsa ntchito njira yodulira makalata. (Motsatira chitsanzo chomwe chili pa tsamba 22)

Werengani mozama ndime yomwe mwadulira-lo. (Motsatira chitsanzo chomwe chili pa tsamba 23)

Filemoni

- 1) Paulo, wandende wa Khristu Yesu, ndi Timoteo mbaleyo, kwa Filemoni wokondedwayo ndi wantchito mnzathu,
- 2) Ndi kwa Apiya mlongoyo, ndi Arkipo msilikari mzathu, ndi kwa Mpingo uli m'nyumba yako:
- 3) Chisomo kwa inu ndi mtendere za kwa Mulungu Atate wathu ndi ambuye Yesu Khristu.
- 4) Ndiyamika Mulungu wanga nthawi zonse, ndi kukumbukira iwe m'mapemphera anga,
- 5) Pakumva za chikondi chako ndi chikhulupiliro uli nacho chakulingana kwa Ambuye Yesu, ndi kwa oyera mtima onse;
- 6) Kuti chiyanjano cha chikhulupiliro chako chikakhale champhamvu podziwa chabwino chili chonse chiri mwa inu, cha kwa Khristu.
- 7) Pakuti ndinali nacho chimwemwe chambiri ndi chisangalalo pa chikondi chako, popeza mitima ya oyera mtima yatsitsimuka mwa iwe, mbale.
- 8) Momwemo, ndingakhale ndili nako, kulimbana mtima kwakukuru m'Khristu kukulamulira chimene chiyenera,
- 9) Koma makamaka ndidandaulira mwa chikondi, pokhala wotere, Paulo nkhalamba , ndipo tsopano wandendenso wa Khristu Yesu;
- 10) Ndikudandaulira chifukwa cha mwana wanga , amene ndambala m'ndende, Onesimo,
- 11) Amene kale sanakupindulirani, koma tsopano watipindulira bwino iwe ndi ine;
- 12) Amene ndi yemweyo ndakubwezera iwe, ndiye mtima weni weni wa ine.
- 13) Ameneyo ndikadafuna ine kumsunga akhale nane, kuti m'malo mwako akadanditumikira ine m'ndende za Uthenga Wabwino.

- 14) Koma opanda kudziwa mtima wako sindinafuna kuchita kanthu; kuti ubwino wako usakhale monga mokakamiza, komatu mwaufulu.
- 15) Pakuti kapena anasiyanitsidwa ndi iwe kanthawi chifukwa cha ichi, ndi kuti udzakhala naye nthawi zonse;
- 16) Osatinso monga kapolo, koma woposa kapolo, mbale wokonedwa, makamaka ndi ine, koma koposa nanga ndi iwe, m'nthupi, ndiponso mwa Ambuye.
- 17) Ngati tsono undiyesa oyanjana nawe, umlandire iye monga ine mwini.
- 18) Koma ngati anakulakwira kanthu, kapena wakongola kanthu, undiwerengere ine kameneko;
- 19) Ine Paulo ndichilemba ndi dzanja langa, ndidzachibwezera ine; kuti ndisanene nawe kuti iwe ndi mangawa anga.
- 20) Inde, mbale, ndikondwere nawe mwa Ambuye: utsitsimutse mtima wanga mwa Khristu.
- 21) Pokhulupilira kumvera kwako ndikulemba iwe, podziwa kuti udzachitanso koposa chimene ndinena.
- 22) Koma undikonzerenso pogona; pakuti ndiyembekeza kuti mwa mapemphero anu ndidzapatsidwa kwa inu.
- 23) Epafra wandende mnzanga mwa Khristu Yesu akulankhula iwe;
- 24) Ateronso, Marko, Aristarko, Dema, Luka antchito anzanga.
- 25) Chisomo cha Ambuye wathu Yesu Khristu chikhale pamodzi ndi mzimu wanu. Amen.

KUDULIRA

NDIME: _____

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

YESAYA 55-ULOSI

- 1) Werengani mawu ochokera pa Yesaya 55 kangapo.**
- 2) Dulirani mawu-wo pogwiritsa ntchito njira yosavuta yodulira malemba.**
- 3) Siyanitsani mitundu ya maulosi yomwe ikupezeka m'ndimeyo.**
- 4) Pezani mfundo yaikulu ya ulosi-wu.**
- 5) Werengani mozama ndime yomwe mwadulira-lo.**
- 6) Pangani mfundo zikuluzikulu za ulaliki omwe mungatenge pa malemba amenewa. Tengani mfundo yoyamba ndipo iwunikireni ndime kwa ndime. Pa mfundoyi, fotokozani ndime zonse za malemba-wa zomwe zikufotokoza mfundoyi. Nkoyenera kufotokoza mawu ndi ziganizo zomwe mwazimvesetsa, mwazitanthauzira komanso zomwe mwazikwaniritsa. Pangani chimodzimidzi ku mfundo zotsatira. Ganizirani nthano zomwe zingakuthandizeni kufotokoza mfundo-zi. (Werengani chitsanzo pa tsamba 45)**

YESAYA 55

- 1) Inu nonse, Inu okumva ludzu, idzani kumadzi; ndi osowa ndarama idzani inu mugule mudyeye; inde idzani, mugule vinyo ndi mkaka opanda ndarama ndi opanda mtengo wake.
- 2) Bwanji inu muli kutayira ndarama chinthu chosadya, ndikutayira malipilro anu zosakhutitsa? Mverani Ine mosamalitsa, nimudyeye chimene chiri chabwino, moyo wanu nukondwere ndi zonona.
- 3) Tcherani khutu lanu, mudze kwa Ine, imvani, mzimu wanu nuzakhala ndi moyo; ndipo ndidzapangana nanu chipangano chosatha, ndicho zifundo zoono za Davide.
- 4) Taonani, ndampereka iye akhale mboni ya anthu, wotsogolera ndi wolamulira anthu.
- 5) Taona, iwe udzaitana mtundu umene sunawudziwa, ndi mtundu umene sunakudziwa udzakuthamangira, chifukwa cha Yehova Mulungu wako, ndi chifukwa cha Woyera wa Israyeli; pakuti Iye wakukometsa.
- 6) Funani Yehova popezeka Iye, itanani Iye pamene ali pafupi;
- 7) Woipa asiye njira yake, ndi munthu osalungama asiye maganizo ake, nabwere kwa Yehova; ndipo Yehova adzamchitira chifundo; ndi kwa Mulungu wathu, pakuti Iye adzakhululukira koposa.
- 8) Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu sizili njira zanga, ayi Yehova.
- 9) Pakuti monga kumwamba kuli kutari ndi dziko lapansi, momwemo njira zanga zili zazitali kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambana maganizo anu.
- 10) Pakuti monga mvula imagwa pansu ndi matalala, kuchokera kumwamba yosabwerera komweko, koma ikhamiza nthaka ndi kuibalitsa, ndikuiphukitsa, ndikuyipatsitsa mbewu kwa wobzala, ndi chakudya cha wakudya.
- 11) Momwemo adzakhala mawu anga amene atuluka m'mkamwa mwanga, sadzabwerera kwa Ine chabe, koma adzachita chimene ndifuna, ndipo adzakula m'mene ndinawatumizira.
- 12) Pakuti inu mudzatuluka ndi kukondwa, ndikutsogozedwa ndi mtendere; mapiri ndi zitunda zidzayima zolimba pamaso panu, ndi mitengo yonse ya m'nthengo idzawomba m'manja mwawo.
- 13) M'malo mwa mithethe mudzatuluka mtengo wa mlombwa; ndi m'malo mwa lunguzi mudzamera mtengo wamchisu; ndipo chidzakhala kwa Yehova ngati mbiri, ngati chizindikiro chosatha, chimene sichidzalikhidwa.

I. MFUNDO YAIKULU:

NDONDMEKO YODULIRA
MALEMBA MOSAVUTA

II. KUDULIRA MALEMBA

1. NDIME _____

2. NDIME _____

III. NDONDOMEKO:

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

MVESETSANI MALEMBA	TANTHAUZO LA MALEMBA	ZOMWE MUNGACHITE POKWANIRITSA MALEMBA

Ndondomeko ya ulaliki

Pogwiritsa ntchito ndondomeko yomwe mwapanga kale pano mutha tsopano kukonza ndondomeko ya ulaliki wanu.

Mutu wa
ulaliki: _____

Bukhu: _____ Ndime _____

I. Mawu oyamba a ulaliki

Yambani ndi nthano, ndakatulo kapena mawu a nthabwala musanayambe kulalikira. Izi zikhale zogwirizana ndi malemba omwe mukufuna kulalikira.

II. Tunthu la uthenga

Potsatira ndondomeko yanu, werengani ndime zonse zomwe mwazisanthula kale.

Tsatirani ndondomeko yanu polongosola uthenga wanu.

ZINDIKIRANI: Si malemba onse omwe ali pansu pa mutu ‘omvesetsa mawu’ akuyenera kutanthauziridwa kapena kukwaniritsidwa.

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

(Pangani chimodzimidzi pa ndime zonse)

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

Ndime _____

O (Kumvesetsa malemba) _____

I (Kutanthauzira malemba) _____

A (Kukwaniritsa malemba) _____

III. Mawu omaliza

Pogwiritsa ntchito mfundo zomwe mwazisanthula kale, mangani nkota mfundo zikuluzikulu za ulaliki wanu ndipo atsogolereni anthu m'mene angakwaniritse zomwe aphunzira.

Zowonjezera

M'MENE MUNGAYAMBIRE NDI
KUTSOGOLERA MAPHUNZIRO A BAIBULO

Kuyambitsa maphunziro a Baibulo chitha kukhala chinthu cha mtengo wapatali kwa gulu komanso mtsogoleri. Ngati simunatsogolerepo gulu, ndi cha nzeru kuyamba pang'ono-pang'ono nkumakula. Yambani kukomana pang'ono pang'ono, monga kamodzi pa sabata kwa mwezi umodzi. Izi zikuthandizani kuphunzira komanso kuyamba kuchita bwino pang'ono-pang'ono. Ngati mutayamba mowirikiza, chidwi chitha kuwachokera anthu ndipo atha kusiya kubwera asanakhwime mokwanira ndipo izi zitha kukufooketsani.

Kodi ndingayitane ndani?

Musanayitane aliyense pempherani. Mukhutitsidwe kuti Mulungu akukonza mitima ya anthu ena omwe ali ndi njala ya mawu Ake. Choonadi ndi chakuti, Mulungu wakhala akukonza mitima ya anthu ena ngakhale inu musanaganize zoyambitsa maphunziro a Baibulo. Mukamapemphera, Iye azabweretsa kwa inu anthu ena omwe muzadziwa kuti nkoyenera kuwayitana. Yambani ndi anthu ochepa, anthu awiri kapena atatu ndi amene mukufuna. Mukayamba kukula m'malemba, gulu nalonso litha kuyamba kukula, koma nkoyenera kuyamba mochepea.

Kodi pakufunika nthawi yambiri bwanji?

Atsogoleri omwe amadziwa bwino zophunzitsa malemba amati nthawi yophunzirira Baibulo isamapyole ola limodzi. Ophunzira ena chidwi chimawachokera ndipo atha kusiya kumabwera ku maphunziro ngati nthawi-yi ikutalika. Sankhani nthawi yokomanira yokomera aliyense wa pa gulu ndipo muzikomana masiku omwe aliyense akusangalala nawo. Nthawi zina mutha kumaphunzira kwa nthawi yotalika pang'ono koma muzidziwa zofuna za gulu.

Kodi ndikonzekere bwanji?

Maphunziro abwino a Baibulo samachitika mwa ngozi-amawakonza mosamala. Choyamba, lorani Mulungu ayankhule mu mtima mwanu mukamaphunzira. Lorani mawu Ake alowe mu mtima mwanu ndikukulalikirani. Chachiwiri dzipatseni nthawi yokwanira yophunzirira mawu a Mulungu kuti muwamvesetse ndi kutha kutsogolera gulu bwino. Ngati mungapange zinthu mwachangu, nkutheka kuti maphunziro-wo sakwaniritsa zomwe Mulungu amafuna kuti akwaniritse. Mukakonzeka bwino ndipo mwagwidwa ndi choonadi cha Mulungu, nkosavuta kuti gulu lanu nalo lipindule ku ichi.

Mukawerenga malemba kangapo, yambani kudulira ndime ndi cholinga chosanthula mfundo. Yang'ani pomwe magawo a mawu ayambira ndi kuthera. Dzifunsemi ngati mfundo yathera apa kapena ikupitirira m'gawo lina. Kodi mfundo yaikulu apa ndi iti?

Mukadulira ndime yanu, yambani kukonza ndondomeko yomvesetsa malemba pogawa mfundo m'mitu itatu: 'kumvetsetsa malemba', 'tanthauzo la malemba' komanso 'kukwaniritsa malemba'. Mukamaliza izi ndi inu okonzeka kuyamba kukonza mafunso othandiza kumvesetsa malemba. Funsani mafunso omwe avumbulutse mfundo yaikulu m'gawo lililonse la malemba. Mafunso anu akhale m'ndondomeko yomwe malemba alili. Kumbukirani kuti tikuphunzira malemba mwa ndondomeko.

Kodi nditsogolere bwanji?

Mukamaliza kukonza mafunso ndi inu okonzeka kutsogolera gulu lanu pa maphunziro. Kumbukirani kuti simuyenera kuziyankha nokha mafunso. Ngati gulu silikumvetsa funso, funsaninso funsola mwa mtundu wina. Nthawi zonse muzitsogolera gulu kuyankha mafunso kuchokera ku malemba.

Kumbukirani kuphunzitsa malemba monga m'mene mungaphunzitsire phunziro liri lonse kuchokera m'bukhu. Lekani malemba aziyankhulire okha.

Kulingalira utsogoleri wanu

Mukamaliza kuphunzitsa dzifunse mafunso ali pansywa kapena pemphani m'Khristu wina m'gulu lanu kukuthandizani kulingalira utsogoleri wanu. Musanatero osamnthokoza Mulungu bwanji chifukwa cha mayankho ena omwe anabwera pa nthawi yamaphunziro mumatsogolera-wa. Ngakhale simukukhutira ndi m'mene maphunziro anayendera, mutha kumnthokoza Mulungu kuti agwiritse ntchito mawu Ake mopambana kwa aliyense amene anabwera ku maphunzoro-wo.

KUKONZEKERA KWANU

- 1. Mukuganiza kuti munakonzekera mokwanira?*
- 2. Kodi munatha kugwira chiphunzitso chachikuru cha malemba?
Munavomereza kuti chiphunzitso chikugwireni?*
- 3. Kukonzekera kwanu m'mapemphero: Kodi mukufuna kusintha zimene mumapempherera mukamakonzekera maphunziro ali nkudza?*

MACHITIDWE ANU

- 1. Mumayembekeza Mulungu kugwira ntchito m'maphunziro?*
- 2. Munawonetsa chidwi kwa anthu payekha-payekha posonyeza kuti mwawalandira ndipo munthu yemwe anali ndi funso kapena vuto akanafuna kuyankhula nanu?*
- 3. Munali okonzeka kuphunzira zinthu zina ku gulu?*

MALO NDI MACHITIDWE

1. *Kodi machitidwe anali omasuka?*
2. *Kodi anthu anali omasuka kupereka maganizo awo ndikutengapo mbali?*
3. *Mumawalimbikitsa bwanji anthu kuti atengepo mbali?*

NTHAWI

1. *Mutatsogoleranso maphunziro pa ndime yomweyi, mungasinthe machitidwe ake?*
2. *Kodi munayamba ndi kumaliza mu nthawi yake monga m'mene munakonzera?*

ZOKAMBIRANA

1. *Lembani ndandanda wa zinthu zomwe mwaphunzira zokhudza kutsogolera gulu:*
 - a) *Gulu lanu linamvesetsa ndondomeko ya zokambirana*
 - b) *Gulu lanu linayang'ana mafunso m'malemba?*
 - c) *Kodi munaziletsa kuyankha mafunso anu monga mtsogoleri? (Koma munatha kugawana nalo gulu apa ndi apo monga chiwalo cha gulu?)*
 - d) *Munasintha mafunsidwe a funso ngati gulu silinathe kulimvetsa?*
 - e) *Munatha kulimbikitsa anthu angapo kuyankha funso limodzi mosiyanasiyana?*
 - f) *Pali chinthu chomwe mungawapemphe Ambuye kuti achitire anthu payekha-payekha zomwe zingawalimbikitse kutengapo mbali pa zokambirana?*
 - g) *Pali munthu wina mukufuna kumuthandiza kuti azitha kutenga mbali pa zokambirana? Kukamba naye pa yekha.*

CHOLINGA

- 1. Kodi zokambirana zinalozera mfundo zikulu-zikulu za m'malemba? Kodi gulu linadziwitsidwa mfundozi kuti anthu athe kuziganizira bwino ndi kuchita zomwe zikuphunzitsa?.*
- 2. Kodi mfundo zikulu-zikulu munazikambirananso pa mapeto pofuna kukumbutsana?*
- 3. Ndi inu okwaniritsidwa kuti maphunziro akwaniritsa zomwe amayenera kutero? Pali anthu ena omwe amawoneka kuti akugwira choonadi pa iwo okha?*

ZINA ZOMWE MUNGALINGALIRE

- ✓ *Lekani malemba kuyankha mafunso omwe abwere osati mtsogoleri*
- ✓ *Yesetsani kukhala pa ndime yomwe mukuwerengayo. Pali nthawi zina zomwe muzafuna kudziwa zina zokhudza ndimeyo koma phunzirani kuyima pa ndime yomwe mukuphunzira*
- ✓ *Khalani pa nsonga ya mfundo yomwe mukukukambirana-nkosavuta kusochema ndikuyamba kukamba zinthu zomwe sizikugwirizana ndi malemba*
- ✓ *Nkoyenera munthu aliyense athandizapo pa kuphunzira kwa gulu. Anthu omwe amayankhula kwambiri aziganizira anzawo ofatsa ndikuwapatsa mwayi kuti nawo atengepo mbali pa zokambirana*
- ✓ *Anthu ena akalowa gulu nkothandiza kukumbutsananso ndondomeko yomwe gulu limatsatira pophunzira malemba.*

Mukamafunsa mafunso perekani nthawi yokwanira kuti gulu lipeze mayankho m'malemba. Nthawi zina gulu lizikhala chete kwa ka nthawi mukafunsa funso. Lisiyeni gulu choncho chifukwa limakhala likufufuza mayankho m'malemba.

Mafunso ambiri azayankhidwa m'njira zingapo, choncho dikirani kuti mayankho onse abwere. Akayankha oyamba, mutha kulimbikitsa gulu kuti lipereke mayankho ake ponenena kuti, "Maganizo abwino, alipo wina amene ali ndi mfundo ina?"

Kumbukirani kuti zokambirana zanu zitha kumayamba mofooka mukamakomana koyambilira, koma zizayamba kuyenda bwino anthu akayamba kudziwana komanso akadziwa bwino lomwe ndondomeko ya kaphunziridwe ka malemba. Kwa ine uku kutha kukhala koyamba kuphunzira malemba mwa mtundu uwu.

Musadandaule ngati mayankho ena akukuwonekerani odabwitsa kapena osagwirizana ndi zomwe mukukambiranana. Kumbukirani kuti Mulungu akugwira ntchito yake ndipo si udindo wa mtsogoleri kukonza mfundo za anthu. Udindo wa mtsogoleri ndi kuyika aliyense m'malemba ndi kuleka malemba-wo kukonza anthu. Pali anthu ena omwe amafuna kumavumbulutsa mavuto. Afunseni kusunga kaye mavuto-wo mpaka pa mapeto pomwe mungakambirane nawo pa iwo okha. Kwaniritsani kukambirana ndi otere pa mapeto.

Nthawi zina pa zokambirana, munthu atha kubweretsa yankho la funso lomwe simunafunse. Kambiranani yankho-lo pa nthawi yomwe labwera osadikira pomwe mufunso funsola. Pofuna kutsindika mutha kufunsanso funsola pa nthawi yomwe mumayenera kulifunsa ndi kukumbutsa gulu zomwe munakambirana kale.

Nthawi zina zokambirana zimautsa chidwi choti mumazazindikira kuti anthu onse akukamba zosiyana ndi mfundo ndipo nthawi ikutha. Mumafuna zokambirana zabwino komanso mumafuna kuti Mulungu aziyankhula kupyolera m'malemba. Mukapatsa gulu theka yokha ya ndime, gulu-lo liphunziraponso theka lokha la mfundo. Phunzirani kubwezera gulu ku mfundo yoyenera pomwe mwawona kuti gulu likusochera ndikupitilira ku funso lina.

Mukamaliza maphuziro aliwonse, limbikitsani utsogoleri wanu podzifunsa mafunso omwe ali pa masamba 127 mpaka 129.

Mulungu amagwira ntchito ku gulu lophunzira malemba lomwe liri ndi anthu ochepa ngakhale lomwe lili ndi anthu ambiri. Koma zawonetsa kuti ngati pa gulu pali anthu opitilira asanu ndi atatu, zokambirana sizikhalanso zaphindu kweni-kweni ndipo china chake chimasowapo. Ngati cholinga chanu ndi kukhala ndi zokambirana zachilungamo, zokuya komanso za phindu m'malemba a Mulungu, nkoyenera kukhala ndi gulu laling'ono. Ngati gulu lakula kwambiri, ganizirani zoligawa magulu awiri ndikuphunzitsa munthu wina kutsogolera gulu linalo.

Magulu a ang'ono angathandize kukuza mpingo, mu uzimu komanso muchiwengerero.

ZINA ZOMWE MUNGADZIWE ZOKHUDZA MAGULU ANG'ONO ANG'ONO

Kumvesetsa m'mene magulu ang'ono ang'ono amagwirira ntchito ndi luso loyenera kwa mtsogoleri aliyense. Nthawi zambiri magulu akamayamba kumene anthu amakhala ndi chidwi koma pasanapite nthawi zinthu zimayamba kubwerera m'mbuyo. Izi zimachitika chifukwa chiyani? Pali zifukwa zambiri monga mtsogoleri osalabadira za ena, kusagwirizana kwa anthu pa gulu komanso kusowa ndondomeko yabwino yakapangidwe ka zinthu.

Ngati gulu lalephera ndiye kuti pali chifukwa chomwe chapangitsa. Koma gulu silingalephere ngati tikutsatira zinthu zina zoyendetsera magulu. Magulu ena amagwira ntchito posalabadira zomwe zimapangitsa magulu kupambana. Magulu otere amapambana pa zochita zawo popanga zinthu zomwe zimathandiza magulu kupambana mosadziwa.

ZOVOMEREZEDWA NDI ALIYENSE NDI MAGANIZO ATHU

Magulu amagwira ntchito pa miyeso iwiri: mfundo zomwe aliyense akugwirizana nazo ndi maganizo a munthu aliyense payekha. Ngati ziwiri-zi sizikuvomerezana ndiye kuti mtsogoleri akhala pa mavuto.

Zovomerezedwa ndi aliyense zimatheka kupyolera pa ntchito yomwe gulu-lo ili nalo, monga kuphunzira Baibulo, mapemphero komanso zokambirana zoyendetsa gulu.

Maganizo a munthu aliyense amawoneka pomwe gulu likomana. Gulu lililonse limakhala ndi anthu omwe aliyense payekha amakhala ndi umunthu, makhalidwe, zofuna komanso zolinga za iye mwini.

Munthu aliyense payekha m'gulu amadzifunsa, “Kodi ine ndili pati m'gulu-li?” Kodi anthu avomereza mfundo zanga? Kodi ndingapange bwanji kuti anthu m'gululi adziwe kuti ndi ine wanzeru, oleza, wauzimu kapena wa makhalidwe ena aliwonse omwe gulu limayika patsogolo. “Kodi anthu andivomereza akawona kuti maganizo anga ndiwosiyana ndi iwo?” Mpaka munthu apeze mayankho a mafunso amenewa, sakhala omasuka kutenga mbali pa zochitika.

Apa ndi pomwe mavuto eni-eni amabwera ndipo nkoyenera kuwonesetsa mwa chidwi zomwe zikuchitika.

Kodi munawona kuti magulu ena sapambana pa chilli chonse? Magulu otere amayamba kuphunzira mawu pa Yesaya 1 koma samamaliza amangolekezera pa ndime yachiwiri. M'malo mokwaniritsa chomwe akonza amapezeka kuti akungokangana, ena akungonena nthabwala, aliyense akufuna kuyankhula nthawi imodzi kapena palibe akufuna kuyankhula.

Gulu lililonse lizawonesetsa mfundo zomwe gulu lonse likugwirizana nazo komanso maganizo a wina aliyense payekha. Magulu omwe amagwira ntchito mosazindikira chomwe akuchita ali pa chiwopsezo cholephera. Pasanapite nthawi magulu otere amalephera kukwaniritsa cholinga chawo.

Ngati mstogoleri mukuyenera kuphunzira kuthetsa kusagwirizana kuli konse komwe kungabuke pa gulu. Phunzirani kutha kuzindikira mwansanga mavuto omwe munthu aliyense ali nawo. Muziyesetsa kuzindikira momwe anthu akumvera, chifukwa anthu ambiri sanena m'mene akumvera pa gulu. Anthu nthawi zambiri samanena kuti " Sindikusangalala ndi m'mene zinthu zikuyendera pa maphunzirowa." Amangosiya kutengapo mbali kapena kumangoyang'ana zomwe zikuchitika kunja. Amakhala akunena m'mene akumvera mosagwiritsa ntchito mawu. Munthu amene akugona akukuwuzani china chake. Nthawi zina munthu atha kukhala kuti wakwiya koma kumanena kuti sanakwiye. Choncho ngati atsogoleri tikuyenera kumamvetsa zomwe anthu akutiwuzwa ngakhale sakutero ndi mawu.

Njira yabwino yodziwa zomwe zikuchitika pa gulu ndi kudzifunsa nokha: "Kodi ine ndikumva bwanji panopa?" Ngati ndakhumudwa, ndakwiya kapena ndikuziteteza ndiye kuti china chake chalakwika. Ngati vuto-lo ndilodziwikiratu, libweretseni poyera ndikukambirana. "Ndikuwona kuti enanu mwakhumudwa, kodi tingakambirane?" Ngati mutakambirana zomwe zikukhudza anthu pa iwo okha zitha kuthandiza gulu kupita patsogolo. Muzazindikira kuti gulu limathandizika kwambiri pomwe likukambirana zinthu zokhudza munthu aliyense payekha.

Mtsikana wina anali olimbikira m'gulu laling'ono lophunzira Baibulo. Amatha kutengapo mbali pa zokambirana zili zonse. Tsiku lina anabwera ndikungokhala phee m'ntheke la maphunzirowo. Mstogoleri anazindikira izi ndipo anayimitsa maphunziro ndikufunsa chomwe mtsikanayo chimamuvuta. Mtsikanayo anayamba kulira ndikuwuzwa gulu-lo kuti mayi ake akudwala kwambiri. Gulu nthawi yomwe linayamba kupempherera mayi-wo ndi kugawana mawu ndi mtsikanayo. Gulu-lo linasinthira kuchoka ku gulu la ophunzira ndikukhala gulu losamalira mwa chikondi. Pa zinthu izi timaphunzirapo zinthu zokhudza miyoyo yathu monga ubale, kusamvana maganizo, chikondi, kukhululuka komanso chilungamo. Timaphunzira m'nkuchita tanthauzo mawu omwe timangowaphunzira m'malemba.

MAUBALE A PA GULU

Anthu akakhala pa gulu, nkosavuta kudziwa mmene angachitire zinthu zina. M'mene amapangira zinthu zina nzothandiza ndipo njira zina nzolepheretsa. Mitundu ya anthu ndi yotere:

Anthu olongolora: Amakhala ndi chokamba pa china chilli chonse

Anthu amanyazi: Sakonda kukambapo pazokambirana

Owonerera: Amawona m'mene zinthu zikuchitikira koma satengapo mbali

Wanthabwala: Amasekesa anthu nthawi zonse

Ophotchola: Munthu yemwe akudziwa zochitika koma amabweretsa mfundo zosagwirizana

Wamakani: Amakhala ndi mfundo zamphavu ndipo safuna kugonja

Wosadziwika cholinga: Amakhala ndi zinthu ku mtima koma sazikamba pa gulu.

KUGWIRA NTCHITO NDI MITUNDU YOSIYANASIYANA YA ANTHU

Anthu olongolora:

Mtengereni pambali ndi kuyankhula naye mosamukhumudwitsa. Musamuchititse manyazi pagulu. “Paulo, ndikufuna undithandize kuti anthu ambiri azitengapo mbali pa zokambirana zathu. Ndimathokoza mfundo zomwe umabweretsa koma undithandize kulimbikitsa gulu lonse kutenga mbali pa zokambirana. Ndikafunsa funso usamakhale oyambakuyankha. Tiyeni tilimbikitse anthu ena kutengapo mbali pa zokambirana ndikukagawana ndi gulu mfundo zawo.

Anthu amanyazi:

Pogwiritsa ntchito dzina lake loyamba, mufunzeni munthu wamanyazi funso loti ayankhe. Izi zizamulimbikitsa kuyamba kutengapo mbali pa zokambirana. Mulimbikitseni akayankha pomuyamikira: “Mwaperekawo ndi maganizo abwino kwambiri.”

Owonerera:

Mufunzeni funso loti limupangitse kuyamba kutengapo mbali pa zokambirana. Nthawi zina anthu amawonerera chifukwa samakhala ndi chikhulupiliro kuti gulu liwavomera. Choncho abweretseni ku gulu mwachikondi.

Wanthabwala:

Munthu otere ndi othandiza pa gulu kupangitsa anthu kukhala omasuka. Koma nthawi zina amatha kupanga nthabwala pa nthawi yosayenera. Ngati nthabwala-zi zikuyambitsa mavuto, m’tengereni munthuyu pambali ndikumuthokoza chifukwa cha mphatso yake yanthabwala. Koma mudziwitseni munthuyu kuti akuyenera kumapanga nthabwala-zo nthawi yoyenera yokha-yokha.

Ophotchola:

Munthu wa mtundu uwu utha kubweretsa mavuto aakulu pa gulu ngati mtsogoleri awasiyilira. Phunzirani kumubwezera munthuyu ku mfundo yomwe mukukambirana. Mutha kupanga izi pomuuzza kuti: Nkhani mukukambayo ndiyosalangatsa koma bwanji tizakambe zimenezo bwino lomwe m’tsogolo muno.” Posamupatsa munthuyo kuyankhapo, tsogolerani gulu pofunsa funso lotsatira.

Wamakani:

Ngati munthu wa mtundu uwu akubweretsa mavuto ku gulu, mtengereni pambali ndikuyankhula naye. Muuzeni kuti mfundo zomwe amapereka ndizofunika ku gulu koma m’dziwitseni kuti nkoyenera kuti azipatsa anzake mwayi ofotokoza mfundo zawo osawasutsa. Ngati mtsogoleri alekelere munthu wa mtundu uwu, zingapangitse anthu kusiya kutengapo mbali pa zokambirana powopa kutsutsidwa. Ngati munthu otere atayambitsa mkangano, mtsogoleri akhazikitse bata ndikupitiriza maphunziro. Liwuzeni gulu ubwino wa mfundo za mbali zones zomwe zimakangana ndikunena kuti anthu ena nawonso ali ndi mfundo zokhwima pa nkhanayi. Awuzeni omwe akukangana kuti asiye ndikupilira ndi maphunziro.

Wosadziwika cholinga chake:

Ngati mutawona kuti munthu wina akulepheretsa maphunziro kuyenda monga m’mene mukufunira, fufuzani chomwe chikumuchititsa munthu-yu kupanga chonchi. Musanapange chilichonse, mupempherereni munthuyu mwakachetechete.

Nthawi zina pemphero ndi lomwe limafunika kuthana ndi vuto lotere. Koma ngati mukuwona kuti nkoyenera kugawana naye mawu munthu otere mutha kumufunsa funso lotere: “Chisomo, lero mwafatsa kwambiri, pali china chomwe chikukuvutani?” Kapena, “Mukuwoneka kuti maganizo anu ali patali lero, pali chinthu chomwe tingapempherere nanu limodzi?”

ZOCHITIKA PA GULU

Zochitika pa gulu zimathandiza kupititsa patsogolo kapena kubwezera m’mbuyo maphunziro. Ngati anthu a pagulu akumva kuti ndiwokulandiridwa komanso chikondi, gulu lizakhala labwino. Izi zizachititsa gulu kupewa mavuto. Munthu aliyense m’gulu amafuna kumva kuti ndiwolandiridwa komanso kuti palibe wina akumuweruza kuti athe kutengapo mbali pa zokambirana. Mavuto amayamba ngati munthu m’modzi akuzimva kuti ndiye ali pafupi kwambiri ndi Mulungu ndipo akuwona chifuniro cha Mulungu. Ngati izi zikuchitika ndiye kuti munthuyo amayamba kuweruza anzake. Ngati titayamba kuziwona tokha kuti ndi ife ochimwa koma Mulungu amatikonda, izi zitiithandiza kusamaweruza anzathu komanso kukhala achilungamo.

Ulaliki ovumbulutsa malemba

Mlembi: Earl Palmer

Ndi chinthu cha mtengo wapatali kukhala nanu pa msonkhano uno. Ndikufuna ndigawane nanu, kuchokera ku ntchito yanga ngati m’busa kufunika kwa maphunziro a Baibulo komanso ulaliki ozama m’malemba mu mpingo. Uwu si ulaliki ngakhale ndili ndi malemba omwe ndikufuna kugawana nanu. Awa ndi malemba ochititsa chidwi ndipo ndigawana nanu malemba-wa pomaliza. Chomwe ndikufuna kuchita ndikupereka umboni wakufunika kwa ulaliki ozama pa malemba.

Ndiyamba ndikukuwuzani mbiri yanga, ulendo omwe ndayendamo kuti ndifike pano. Ndikuwona kuti ndichoneyera kuti mudziwe m’mene chidwi changa chotumikira chinakhazikika pa mpingo omwe ndikutumikira lero wa First Presbyterian ku Berkeley komanso mipingo ina yomwe ndinakhazikitsa ndisanabwere kuno, ku Manila komanso ku Seattle. Ndikhulupilira kuti ndikatero mumvesetsa m’mene ndasinthikira mu uzimu chomwe ndi chinthu zofunikira kwambiri pa utumiki.

Ndiine m’badwa ya ku California ndipo ndinakulira pafupi ndi phiri la Shasta. Ndinakulira m’banja losangalatsa, lachiyembekezo komanso lolimbikitsa komanso losalimbikira mapemphero. Ndinasiya kupita ku tchalichi nditatsala pang’ono kumaliza sukulu ku sekondale ndipo sindimapita ku tchalichi zaka ziwiri zoyamba ku University. Mapemphero sanali gawo la moyo wanga.

Ndili chaka chachiwiri ku koleji ndimagona m’phala yotchedwa Barrington Hall pa kolejipo yomwe ndi mphala yomwe mumachitika zinthu zodabwitsa mpaka pano. Tinali ndi mbiri yoti zomwe zimachitika m’phalayi ndi zosagwirizana ndi chikhalidwe cha chi-Mereka. Anyamata mazana awiri ndi makumi asanu amagona m’phala imeneyi ndipo ine ndinafika posankhidwa mtsogoleri wa mphala-yo. Ndinadutsa pa mphalayi tsiku lina lake; idakalibe pomwepo. Pongofuna

kukupatsani chithunzi-thunzi, pakadali pano mphala-yi anayilembalemba chifukwa anthu sakusangalala ndi zomwe zimachitika kumeneko. Pa chipata analembapo mawu akulu akulu oti “Uchoke pano.”

Mkati mwa chaka chachiwiri ku koleji m’nzanga anandiyitana kupita ku gulu lophunzira malemba a m’Baibulo. Gulu-li limakoma kamodzi pa sabata m’chipinda chogona cha m’modzi mwa ophunzira ndipo amaphunzira mozama malemba ochokera m’chipangano chatsopano. Pa tsikuli anakomana kwa ola limodzi kukambirana mozama malemba a m’chipangano chatsopano. Ndimakumbukirabe zomwe ndimagaliza pomwe ndinakhala nawo koyamba pa maphunzirowa.

Ndinali odwabwa kuwona anyamata a msinkhu wanga akuwerenga ndi kutanthauzira malemba a m’chipangano chatsopano ngati akulu akulu ndikumambirana mozama komanso mokhwima. Chinali chinthu chodabwitsa kwambiri.

Ndinalibe Baibulo nthawi imeneyo moti ndimawerenga Baibulo ndi munthu wina. Ndinachita chidwi kwambiri moti ndinati: “Ndikufuna ndizikhala nawo pa zokambirana za gulu lino.” Ndinakagula Baibulo langa sabata yomweyo. Tinali ndi ma Baibulo ku nyumba koma ine sindinatengeko pomwe ndimapita ku koleji. Posadziwa kuti ma Baibulo amanthauziridwa mosiyana ndinakagula Baibulo lolakwika la King James Version. Sabata yotsatira nditapita kumaphunziro anandiwuza kuti “Sitikugwiritsa ntchito mtundu wa Baibulo limenelo, tikugwiritsa ntchito Baibulo la Revised Standard Version.” Ndinabwerera kukagula Baibulo loyenera. Sindinali m’khristu kale apa koma ndinagula kale ma Baibulo awiri sabata imodzi. Ndinagula Baibulo la Revised Standard Version ndipo ndinayamba kukhala nawo pa zokambirana za gululi.

Chaka chomwe ndinayamba kukhala nawo pa maphunziro a Baibulo ndinakakhala nawonso pa msonkhano wachitsitsimutso omwe unachitika ku Lake Tahoe, komwe alaliki anali, Edward John Carnell ndi Robert Boyd Munger. Ndimakumbukirabe m’mene moyo wanga unasinthira pomwe Robert Munger anati: “Mukakhutitsidwa ndi kukhulupirika kwa Yesu Khristu ndipo ndi inu okonzeka kukhulupilira m’kukhulupirika Kwake, ndi inu okonzeka kukhala m’Khristu. Amanena mawuza kwa gulu lonse osati kwa ine ndekha komabe ngakhale zinali choncho ndinamva mu mtima kuti akuyankhula mawu-wa kwa ine.

Ndimakumbukira kuti ndinapita ku nyanja ndikupanga chisankho choti ndikufuna kukhulupilira m’kukhulupirika kwa Yesu Khristu.

“Ndikathandiza anthu kuwerenga ndikumvetsa malemba mozama, malemba-wo azawatembenuza anthu mwa iwo okha”

Izi zinachitika koyambilira kwa chaka changa chachiwiri ku koleji. Nditabwereranso ku koleji, ndinakula mu uzimu mwansanga. Ndinapitiriza kukomana ndi gulu lophunzira malemba komanso monga ndanena kale ndinakhala mtsogoleri wa m’phala ya Barrington komanso mtsogoleri wa magulu

onse ophunzira malemba pa koleji-yo. M'mene ndimapanga izi nkuti ndikutengapo mbali kwambiri pa zochitika za gulu lophunzira malemba laling'ono lija.

Tinawona zodabwitsa zikuchitika pomwe ndinali m'chaka chomaliza ku koleji. Tinawona anyamata a m'mphala yomwe ndimagona akusinthika kukhala a Khristu pafupi fupi mnyamata m'modzi sabata iliyonse. Zinangochitika mwa zokha. Anyamata amangosintha mwa iwo okha ndipo Mulungu analemekeza utumiki uwu.

Mkati mwa chaka changa chomalizachi ndinakhudzidwa kwambiri ndi zomwe zimachitika m'gulu lophunzira malemba moti ngakhale cholinga changa chinali chokhala kadaulo wa malamulo kapena ndale ndinapereka umboni kwa mtumiki Robert Munger kuti: “Ndikumva mu mtima mwanga chikoka chodzakhala mtumiki, ndingakwanitse bwanji izi?” Anandiyankha, “Osalemba kalata yofunsa malo ku koleji ya utumiki ya Princeton bwanji?” Choncho ndinalimba kalata ku kolejiyi ndipo ndikukhulupirira kuti ndinali ophunzira osazama kwambiri pa malemba yemwe kolejiyo idatenga.

Mpingo wa First Church ku Berkeley unakonza zoti ndizikagona chipinda chimodzi ndi Lynn Bolick yemwe anali ozama pa malemba ndipo anandithandiza kwambiri m'chaka changa choyamba ku Princeton. Ena akufuna kwabwino ananditumiza ku msonkhano wa chitsitsimutso ku Star Ranch ndisanakayambe sukulu ku Princeton. Nditapita ku Princeton, moyo wanga unasinthika kwambiri. Ndinazindikira zinthu zambiri zomwe zinandilimbisa pa uzimu. Ndinadziwananso ndi John A. MacKay yemwe ndi mlaliki wa mtengo wapatali yemwe ndimam'dziwa. Ndinakhalako ku Princeton zaka zitatu kenaka ndikukayamba utumiki. Koma zomwe zinachitika m'moyo mwanga ku mphala ya Barrington zinasintha moyo wanga kwambiri.

Pomwe ndinali ku Princeton, amatituma kumayenda m'magulu kukalalikira mawu, zomwe ine sizimandisangalatsa. Ndimawona ngati sichinali mwa ine kumakawerenga mawu m'machalichi, kuyankhula ndi achinyamata ndikumakhala pa nkhomaliro ndi mabanja osiyasiyana. Timayimilira sukulu ya utumiki ndipo timagwira ntchito yathu bwino. Ndinapanga izi kanayi kenaka ndinafooka ndikusiya. Koma ndisanasiye ndinapita ndi gulu langa ku Jeckintown pafupi ndi ku Philadelphia ndipo ndinadwa nkhomaliro ndi banja la Kelly. Mwana wa mwamuna wa banjali dzina lake Glen anali m'chaka choyamba ku Koleji ya ukadaulo ya Princeton ndipo anali ku nyumba-ko pa nthawiyo. Mukakamba za nkhomano zokonzedwa ndi Mulungu, ine ndimazikhulupilira.

Ndinamuuza Glen kuti, “Uli pa koleji ya ukadaulo ya Princeton, ine ndili pa koleji ya utumiki ya Princeton. Zosangalatsa-tu izi, tizikakomana tikabwerera. Iye anagwirizana nane. Sabata yotsatira titabwerera tinakomana ndipo ndinamuuza, “Glen, pomwe ine ndinali ku Berkeley ndimakomana ndi gulu lina lake nkumaphunzira limodzi malemba ndipo zinandithandiza kwambiri. Kodi iwe ndi anzako mungakhale ndi chidwi choyambitsa gulu langati ili?” Iye anati, “Ndikamufunse mzanga amene ndimagona naye chipinda chimodzi.” Uku kunali kuyamba kwa gulu lophunzira malemba ku koleji ya ukadaulo ya Princeton.

Magulu ambiri otere anabadwa pa kolejiji moti nthawi ina yake ndimathandiza magulu asanu ndi awiri omwe amandipempha kutero. Uwu unali utumiki wanga m'zaka zitatu zomwe ndinali pa koleji ya utumiki ya Princeton. Magulu-wa amakomana nthawi zosiyanasiyana, ena amakomana 10 koloko usiku, 6 koloko m'mawa kapena 4:30 masana ndipo amakomana kwa ola limodzi. Zokambirana zimatsatira ndondomeko yomwe timatsatira nthawi yomwe ndinali ku Berkeley kusanthula malemba kuchokera m'mabukhu osiyasiyana a chipangano chatsopano. Masabata ena Mtumiki Paulo amapambana nthawi zina amagonja koma izi sizimandikhumudwitsa. Ndimapitiriza kuwerenga malemba ndi ophunzira ena ndikumvesetsa chomwe amalemba akutanthauza. Ndinazindikira chomwe ndinazindikira kale ndili ku Barrington. "Ndikathandiza anthu kuwerenga ndikumvetsa malemba mozama, malemba-wo azawatembenuza anthu mwa iwo okha"

Maguluwa ndimawatchula kuti magulu ophunzira mawu pofufuza. Sindimakonda kuwatchula kuti "Magulu ophunzira malemba mwachitsitsimutso. Nthawi ina ndikuyankhula ndi atsogoleri a m'magulu ochokera m'makoleji a ukadaulo osiyanasiyana ndinawauza kuti, "Musamatchule magulu anu kuti ndi achitsitsimutso, muziwatchula kuti ndi ofufuza." Cholinga chotengera ku gulu lophunzira malemba katundu wapadera ndi chiyani? Tiyeni tiphunzire malemba mwa cholinga chake ndipo tisiye Mulungu kutsitsimutsa anthu ngati Wasankha kutero. Masiku ano, magulu ophunzira malemba m'makoleji aukadaulo ku mpoto kwa California amatchula magulu awo, magulu ophunzira malemba mofufuza.

Ndinawona achinyamata angapo kusinthika kukhala a Khristu kupyolera m'magulu ophunzira malemba ku Princeton. Sindidawaumirize kukhala a Khristu, zinangochitika. Izi zinasintha machitidwe anga a utumiki kwambiri. Ndikukutsimikizirani kuti m'utumiki wanga ku Seattle, ku Manila komanso ku Berkeley ndimagwiritsa ntchito njirayi: Ndikathandiza anthu kuwerenga ndikumvetsa malemba mozama, malemba-wo azawatembenuza anthu mwa iwo okha. Izi zinanditula katundu wambiri ndipo sindimayenera kukhala ochenjera kuti anthu asinthike. Chomwe ndimapanga ndikuthandiza anthu kuti awerenge ndikumvesetsa malemba, ngakhale izi nthawi zina zimafuna ukadaulo wapadera kuti zitheke. Ndinakhulupilira kuti utumiki wabwino ndiomwe umayamba ndi malemba. Osayamba ndi mafunso achikunja kenaka ndikuyesa kupeza mayankho ake m'Baibulo, koma yambani ndi choonadi cha malemba ndikudziwitsa anthu za choonadi chimenechi.

Bukhu lomwe Helmut Thielecke analemba akuwonetsa kusiyana kwa utumiki wa Paul Tillich ndi Karl Barth. M'bukhuli iye akutiwonetsa kuti Paul Tillich amayamba ndi chikhalidwe cha dziko kenaka ndikufunsa mafunso a cholinga cha moyo pamapeto ake ndikuwunikira zomwe malemba anena pa izi. Koma Thielecke amayamba ndi malemba kenaka ndikuwonetsa m'mene malemba akugwirizana ndi zochitika m'moyo tsiku ndi tsiku. Karl Barth akupereka chitsanzo cha bukhu lomwe iye analemba mogwirizana ndi Martin Niemoller komanso Wilhelm Niemoller m'chaka cha 1934. Ndizosangalatsa kuwona kuti gawo lililonse la bukhu limayamba ndi malemba kenaka kutanthauzira malemba-wo ndizochitika za mdziko. Mwachitsanzo, malemba omwe akupezeka pa Yohane 14: "Ine ndine njira," Mawu oti "Ine" akuwonetsa kuti njira yolalikira yoyenera patsogolo izakhala yolalikira podzera kumvesetsa malemba mozama.

Ndinakhutitsidwa kuti kuphunzira Baibulo ndi njira yoyenera yomvetsa malemba ndipo moyo wanga unatenga njira imeneyi.

Ndinakhutitsidwa kuti chitsitsimutso chimakula kuchokera m'kupunzira malemba mofufuza choonadi pomwe sukudziwa kuti ukulalikira. Ulaliki wanga wagona mukumvesetsa malemba pa ubwenzi, m'makomo mwathu. Anthu ambiri ku Berkeley omwe analandira chi-Khristu anachokera m'magulu ophunzira malemba, opemphera komanso m'maubale omwe anthu amawona m'mene Khristu amakhallira komanso chikondi chomwe amagawana. Izi zimapangitsa kuti chidwi chawo chikule pa chi-Khristu ndipo pamapeto pake amasintha kukhala a Akhristu.

Pamapeto ake ndinakhutitsidwa kuti njira yatanthauzo yolalikira komanso kuphunzitsa izakhala kupyolera kuvumbulutsa malemba a m'Baibulo. Ndikukhulupilira ndikoyenera kuti ndikuwuzeni tanthauzo la kuvumbulutsa malemba. Ndasintha pang'ono tanthauzo-li kuchokera pa nthawi yomwe ndinalemba za ichi. Pa nthawi imeneyo ndinalemba tanthauzo la kulalikira movumbulutsa malemba kuti ndikulalikira kosiya malemba a m'chipangano chakale kapena chatsopano kuzitanthauzira okha poperekera umboni wa uthenga wabwino wa Yesu Khristu ndikuzindikiritsa anthu za choonadi cha uthenga umenewo m'chiyankhula cha masiku ano. Ulaliki si kungonena zomwe mawu akunena zokha ayi, mukuyenera kutanthauzira zomwe mawu-wo akutanthauza.

M'mene ndkuwonera, izi zikutanthauza kuti mlaliki kapena mphunzitsi afotokozere zomwe malemba akutanthauza ndimomwe izi zikugwirizana ndi utumiki. Ndikuwuzeni zomwe ndimawona kuti ndi zofooka za ulaliki walero. Ndikuwona kuti pali zofooka pa ulaliki ndi uphunzitsi m'mipingo masiku ano. Ndikukhulupilira kuti zofooka izi zili m'magulu awiri. Gulu loyamba ndi zofooka zomwe zabwera chifukwa cha kuchuluka kwa ulaliki ogwirizana ndi mutu umodzi. Ndikukhulupirira kuti ulaliki wambiri masiku ano m'mipingo umagona pa mutu. Ndikufuna kutanthauza kuti masiku ano alaliki amalalika ndi cholinga chophunzitsa mfundo za chipembedzo koma anthu omvetsera sapatsidwa mwayi owona m'mene mlaliki wavulutsira chiphunzitsi m'malemba. Amagowuzidwa izi ndi mlaliki kapena mphunzitsi nati, "Izi ndiye zomwe tikhulupilira." Samawona komwe chiphunzitsi chikuchokera kapena sapatsidwa mwayi ovumbulutsa chiphunzitsi pa iwo okha. Amagowuzidwa ndipo uku ndi kufala kwa ulaliki ogwira mutu wa chiphunzitsi. Mlaliki amawauza kuti, "Mulungu amakukondani." Samapeza chikondi-chi m'malemba, samawona pomwe chikondi-chi chikuchokera m'malemba. Amagowuzidwa.

Ndikuwona kuti uthenga wabwino omwe amalalikira alaliki atsopano umachokera malo atatu:

- 1) Choyamba ndi zomwe mlaliki kapena mphunzitsi zikumukhudza. Chomwe mphunzitsi kapena mlaliki akuwona kuti ndi chimene Mulungu akufuna kuti anthu amve: izi ndi zomwe mlaliki akuwona malinga ndi njira yomwe wayenda ndi Mulungu.*
- 2) Chachiwiri ndi zomwe mlaliki akudziwa kapena wakhala akuwona. Ndili okhudzidwa ndi njira yatsopano yakalalikidwe yomwe sukulu zambiri za*

ubusa ku Amerika zikulimbikitsa, zoti mlaliki azikamba za mbiri yake yomwe ingathandize kulalikira uthenga wabwino kwa anthu. Ichi chikutanthauza kuti zomwe mlaliki wadutsamo sabata imeneyo ndi pomwe ulaliki umachokera. Ngati mlaliki ndi odziwa kufotokoza nkhani ndiye kuti anthu ambiri alandira uthenga wabwino.

- 3) *Chachitatu chomwe ndikuwona ngati ndichoopsa kwambiri ndi chomwe ndikuchitchula kuti choonadi cha chi-Khristu chomwe aliyense akuyenera kuchidziwa koma palibe amene anachivumbulutsa. Tonse timadziwa choonadi koma zinthu zimathera pomwepo. M'Khristu ongobadwa kumene sakudziwa kuti choonadi chimachokera pati?*

Zonsezi zimayambitsa mavuto apadera. Luther anakhudzidwa kwambiri ndi uthenga omwe uli kunja kwathu. Uthengawu ungaphunziridwe ndikufufuzidwa. Ichi ndi chikhulupiliro chakalekale. Mulungu anayankhula ndipo amamveka. Koma ichi ngati sichikutuluka poyera, uthenga umadalira zomwe mlaliki wadutsamo. Nachi chitsanzo.

Zaka zingapo zapitazo, ine ndi banja langa tinali pa ulendo zomwe zinatipangitsa kulephera kupita ku tchalichi, choncho timamvera mlaliki pa wailesi. Mlaliki analengeza kuti alalikira pa mutu wa chiyembekezo kuchokera pa mawu omwe akupezeka pa Aroma 8. Izi zinandisangalatsa chifukwa ndimakonda bukhu la Aroma maka-maka Aroma 8. Mawu amene anawerenga anali okhudza m'mene Mulungu anakhadzikitsira malire a chilengedwe. Chiyembekezo chinali choti mawu anena kuti Mulungu anakhazikitsa malire a chilengedwe 'pachigamulo' koma Paulo anadabwitsa owerenga ake ponena kuti anakhazikitsa malire ndi 'chiyembekezo'. Apa ndi pomwe mawu oti 'chiyembekezo' akuwoneka. M'busa anawerenga mawuwa koyamba kwa ulaliki wake ndipo kunena zoona ndinakhudzidwa kwambiri ndi malemba awa. Anawerenga malemba-wa bwino kwambiri ndipo izi zinandipangitsa kukhala pafupi ndi wailesi kuti ndimvesetse bwino lomwe.

M'busa analalikira mopereka chiyembekezo mophatikiza ndi nkhani zifupizifupi za mbiri ya moyo wake. Mlaliki anakamba za zinthu zosiyanasiyana zomwe zimachitika m'moyo mwake ndi zina zomwe zinamchitikira. Mlaliki anakamba chinthu china chomwe chinandikhudza kwambiri mpaka kugwetsa misozi. Mlaliki anagawana nafe zinthu zambiri ndipo pamapeto pake amalalika ndi pemphero.

Sindinafuno kukamba zambiri koma ndinali okhumudwa. Palibe nthawi ina iliyonse mu ulaliki wake omwe anakambapo za mawu ochititsa chidwi amene anawerenga bwino lomwe pa Aroma. Palibe pomwe analola mawu-wo kuzifotokoza okha mu ulaliki wake-wo. Mawu-wo sanathandizire chilichonse pa ulaliki-wo. Ulaliki unasanduka nkhani ya mbiri ya mlaliki ndi momwe anaphunzirira chiyembekezo m'moyo mwake.

Mwana wanga wamkazi Anne anandifunsa, “Bambo, mukuganiza bwanji za ulaliki umenewu?” Ndimafuna nditanena zabwino za ulalikiwo chifukwa alaliki tikuyenera kuvomerezana. Ndinati, “Ndikuuza chinthu chimodzi Anne. Chinthu chimodzi chomwe mlaliki ananena chinandikhudza kwambiri.” Ichi chinali chilungamo koma mwana wangayu sanakhutitsidwe ndi zomwe ndinanenazo ndipo anati, “Bambo, ine ulalikiwo sunandisangalatse.” Nditamufunsa chifukwa chomwe sunamusangalatse anandiyankha zomwe sindizayiwala. “Chomwe chinalakwika ndi ulaliki umene-wu ndi choti mlaliki akutiwuzwa kuti tikhale ndi chikhulupiliro chifukwa iye ali ndi chikhulupiliro.” Uwu unali uthenga wa mlaliki osati uthenga wabwino.” Anne wakhala nawo m’magulu ambiri ophunzira malemba. Waphunzira kwa zaka ziwiri zomwe Paul Byer analemba zokhudza uthenga wabwino wa Marko komanso zomwe analemba za Habakuku. Choncho Anne sanali okonzeka kuvomerezana nane chifukwa wakhala akuwona uthenga wabwino ukutuluka m’malemba.

“Kulalikira sikungonena zomwe mawu akunena: mukuyenera kutanthauzira zomwe malemba akutiwuzwa”

Anne anakhumudwanso chifukwa malemba sanapatsidwe danga lolankhula pa iwo okha. Awa anali mawu achiyembekezo omwe Paulo analemba koma Paulo sanapatsidwe mwayi oyankhula mawu-wa. M’malo mwake mlaliki anangotiuza nkhani za mbiri yake. Uku kunali kukamba nthano osati kulalikira.

Panalibe chinthu chimodzi chomwe sindimagwirizana nacho m’uzimu. Koma kufooka kwa ulaliki uwu ndi koti anthu omwe anawumvera sanapatsidwe mwayi owona ndi kuzindikira chiyembekezo chomwe chinali m’malemba, mu uthenga wabwino. Anangomva kuchokera mu zinthu zomwe zinachitika m’moyo mwa mlaliki.

Ndikufunsi funso lalikulu. Kodi zinthu zina zake zitachitika m’moyo mwanu sabata ino mwina zokhudza Mzimu Woyera, kapena maloto kapena masomphenya, mungazalalikire za izi pasabata? Ngati si inu a mipingo yosinthika simunachite izi. Muzikhala othokoza pa zomwe zikuchitika m’moyo mwanu koma lalikirani uthenga wabwino. Uthenga wabwino ndi zochitika m’moyo mwanu ndi zinthu ziwiri zosiyana. Zochitika m’moyo mwanu zitha kuchitira umboni uthenga wabwino ndipo ngati alaliki tigwiritse izi pofuna kufotokoza kuwonetsa ubale wathu ndi anthu. Ichi ndiye cholinga cha nkhani za m’moyo wathu. Koma uwu si uthenga. Ngati nkhani zokhudza moyo wathu zisanduke uthenga, ndiye kuti nkhanizo si mlumiki wa anthu ku malemba. Mapeto ake zichititsa anthu kubwerera mbuyo.

“Uthenga wabwino ndi zochitika m’moyo mwanu ndi zinthu ziwiri zosiyana. Cholinga cha ulaliki ndikulimbikitsa kuti anthu amve uthenga ndi kuti uthenga-wo ukhazikike m’mitima yawo”

Kodi nanga zimakhala bwanji pa nthawi yomwe mulibe chiyembekezo kapena simukulabadira chilichonse? Zochitika m'moyo kapena nkhani za mbiri yanu ndizosakwanira.

Tithokoze Mulungu chifukwa cha Mayi Tereza, koma Mayi Tereza si uthenga wabwino. Chikondi chomwe Mayi Tereza amawonetsa anthu ku Calcutta si uthenga wabwino. Ndi umboni wabwino wa uthenga wabwino, koma uthenga wabwino ndi Yesu Khristu mwini.

Uthenga wabwino uli m'malemba ndipo chimakhala chinthu chosangalatsa munthu akavumbulutsa uthenga wa chiyembekezo kuchokera m'malemba ndipo nkhani za m'moyo wake zikugwirizana ndi uthengawo.

Ndikupatseni chitsanzo china cha vuto limeneli. Pali abusa ambiri omwe sangalalikire pamapeto pake nkumakamba zoonadi zeni zeni za Chikristu. Izi zimachitika chifukwa abusa-wa amafuna kuti anthu apange chisankho pamapeto pa ulaliki. Choncho mlaliki amalalikira bwino lomwe kuwapatsa malemba danga lozitanthauzira okha. Pamapeto pake mlaliki amapezeka kuti akukamba zinthu zomwe sizili m'maganizo ake kapena m'maganizo a anthu omvera. Panthawiyi anthu amakhala akukonzeka zoweruka akuchita kudziwiratu kuti ulaliki ukunka kumapeto.

Muikamamaliza kulalikirira zomwe malemba akunena, lekezani pomwepo. Monga momwe ndanenera kale, ndikukhulupilira kuti vuto lalikulu la ulaliki masiku ano ndikudalira mutu womwe mlaliki wasankha. Mogwirizana ndi vuto ili ndi vuto lakusowa utumiki pomwe zomwe timagawana ndi anthu zomwe tavumbulutsa koma sitipanga izi motsogozedwa ndi Mulungu. Mlaliki nthawi zambiri amanena kuti, "Ndawauza anthu choonadi. Ndawauza anthu uthenga wabwino." Koma kumbukirani kuti kungowuza anthu choonadi sikutanthauza kuti mwawatanthauzira chomwe choonadi-cho chikunena. Cholinga cha ulaliki ndi kuwuzwa anthu chowonadi chomwe chikhazikike m'mitima yawo. Pamapeto pake zimatengera zodabwitsa za Mzimu Oyera kuthandiza kuti uthenga wabwino ukhadzikike m'mitima ya anthu.

Njira yabwino yowonesetsa kuti mfundo yakhadzikika m'mitima mwa anthu ndikulola anthu-wo kuzindikira chowonadi pa iwo okha. Cholinga cha ulaliki ovumbulutsa ndikuthandiza munthu kuwona iye yekha chomwe malemba akunena, "Ndapeza pomwe chowonadi chilli m'malemba. M'njira ina cholinga cha ulaliki ovumbulutsa ndikuthandiza malemba m'chipangano chakale kapena chatsopano kuziyankhulira okha.

Kaya mukutsogolera gulu lophunzira malemba kapena mukulalikira, ndikuganiza kuti iyi ndiye njira yolalikira kapena kuphunzitsa yomwe mpingo ukusowa. Ndivomereze kuti si ulaliki okha omwe mpingo umafuna koma ndikukhulupilira kuti kulalikirira uku ndikumene mpingo ukusowa. Ndikulimbikitseni kuti inu monga abusa muzikhala nawo pa magulu ophunzira malemba. Ndinauza ophunzira anga lero kuti, "Lamulo loyamba lomwe mungatsatire ngati mukufuna kukhala munthu odziwa kupereka uthenga ndikupewa kukwezekedwa mpaka kufika pokhala munthu olephera. Tizipewa ichi mu utumiki. Musazilore nokha kukwezedwa

kuposa malo omwe munaphunzira malemba. Ndikukulimbikitsani kuti muyambitse magulu ophunzira mawu mofufuza m'miyoyo yanu komanso m'chalichi.

Pamapeto ndikulimbikitsa kuti muzilalikira movumbulutsa malemba nthawi zones. Ndikukhulupilira kuti ulaliki ovumbulutsa malemba wabwino ndi pamene mlaliki aganizira mozama malemba limodzi ndi anthu kwa nthawi yaitali, kupyolera mabuku osiyanasiyana komanso kupyolera m'Baibulo. Limbikitsani anthu omwe mukawalalikira kukambirana nanu. Ndili ndi malemba ochokera m'kalata yachiwiri yomwe Paulo analemba Atesalonika. Mabuku oyamba omwe Paulo analemba m'chipangano chatsopano anali makalata omwe anatumiza kuchokera ku Atene kupita ku tchalichi ku Tesalonika, panthawiyo linali likulu la Makedinoya. Analemba makalata awiri ku mpingo-wo chifukwa anthu kumeneko anazunguzika ndi mfundo zingapo, komanso anawathokoza powapempha chithandizo. Malemba-wa akupezeka pa 2 Atesalonika 3: Chotsatira, abale, mutipempherere, kuti mawu a Ambuye athamange, nalemekezedwe, monganso kwanu." Ndimakonda mawu awa; ichi ndiye chodabwitsa cha ulaliki. Chodabwitsa cha malemba ndi chakuti Mzimu Oyera uzatigwiritsa ntchito ndipo tizipempherera ichi nthawi zonse.

Mbusa Earl Palmer wakhala akutumikira mpingo wa First Presbyterian ku Berkeley, California kuchokera mchaka cha 1970 atatumikira m'mpingo ina ku Phillipines, Seattle komanso Washington. Mbusa Palmer walembe ndikutsindikiza mabuku ambiri a chi-Khristu. Mbusa-yu analandira digiri yake ya ukadaulo kuchokera ku koleji ya ukadaulo ya California, ku Berkeley ndipo analandira digiri ya udotolo wa utumiki kuchokera ku koleji ya utumiki ya Princeton.

Nkhaniyi anayitsindikiza mu nyuzipepala ya utumiki m'mwezi wa December chaka cha 1985. Tayisindikiza m'bukhu lino ndi chilolezo cha Fuller Theological Seminary.

*KUPHUNZIRA MALEMBA A M'BAIBULO
M'mene mungawerengere mawu a Mulungu ndikuwamvetsa*

M'malo mwa anthu onse kuno ku Intensive Care Ministries komanso m'malo mwa ine mwini, ndikufuna ndikuthokozeni. Mulungu akudalitseni pomwe Mzimu Oyera ukukuvumbulutsirani tanthauzo la mawu ake.

Mbusa Dan Finfrock

Zaka 20 zophunzitsa atsogoleri ndikukuza okhulupilira

“Kuphunzira malemba mozama ndi njira yomwe abusa a mpingo wa Calvary Chapel amaphunzirira ndi kuphunzitsira malemba. Bukhu ili ndilothandiza kwa anthu omwe akufuna kuphunzira njira-yi.”

PASTOR CHUCK SMITH

Calvary Chapel-Costa Mesa, CA

Anthu ongobadwanso kumene, atumiki ochokera m'madera ena, ophunzira m'sukulu za sekondale komanso abusa amagwirizana kuti nthawi yomwe anayika m'maphunziro awo inali yopindulitsa ndipo amadabwa kuti njira iyi imachedwa kuti.”

PASTOR LLOYD PULLEY

Calvary Chapel Old Bride, Old Bridge, NJ

“Bukhuli tinaligwiritsa ntchito ku magulu athu ophunzira malemba m'sukulu m'dziko la India. Ophunzira ndi abusa apindula kwambiri ndi maphunziro-wa.”

K.P. YOHANNON

Oyambitsa wa Uthenga wabwino wa ku Asia.

“Dan anaphunzitsa njira iyi kwa abusa athu ndi ophunzira pa sukulu ya utumiki ku Colombia. Izi zinasintha moyo wawo ndi njira za m'mene amaphunzirira Baibulo. Ngati mumakonda kuphunzira malemba, ndikukulimbikitsani kuyesa kugwiritsa ntchito njira iyi.

MBUSA RAUL RIES

Calvary Chapel-Golden Springs, Diamond Bar, CA

P.O. Box 109, Mentone, CA, 92359, USA

(909) 798-0451

www.icmbible.org